BUKU LA UMEMBALA WA MPINGO WA NAZARENE

BUKU LA UMEMBALA

WA

MPINGO WA NAZARENE

Buku La Umembala WA

Mpingo Wa Nazarene

Church of the Nazarene Manual 2009 – 2013 Mofotokozedwa ndikuchepetsedwa ndi Neville Bartle.

© Global Nazarene Publications
Church of the Nazarene

Lotsindikizidwa ndi
Church of the Nazarene
P.O. Box 16973
Suva, Fiji

Kutsindikizidwa ndi Kukonzedwa Mololezedwa ndi
Africa Nazarene Publications
P.O. Box 1288
Florida
1710
Republic of South Africa

ISBN -978-0-7977-1145-7

Church Member's Handbook
Chichewa

Za Mkatimu

Ngodya Za Chikhulupiliro Chathu ……..……5

Mawu Oyamba……..7

Nsanamira za chikhulupiliro chathu.……8

Malamulo a Mamembala…….…..18

Pangano la Moyo wa Chikhiristu…….20

Kapangidwe ka Mpigo…….30

Mpingo…….…32

Msonkhano wa Chigawo……..…..……..44

Msonkhano Waukulu Wa Mpingo Wonse..…….54

Mtumiki…….……60

NGODYA ZA CHIKULUPILIRO ZA MPINGO WA NAZARENE

Tikanena kuti “ngodya” tikutanthanza zinthu zikuluzikulu zomwe chikhulupiliro chathu chidakhazikikapo monga mpingo wa Nazarene.

1. NDIFE AKHRISTU

Ndife a khristu, olunzanitsidwa ndi okhulupilira onse mu kulalikira Yesu Khristu kuti ndi Mbuye. Timakhulupilira kuti Mulungu anatikonda zedi motero kuti adapereka mwana wake mmodzi yekhayo, Yesu kuti akhale mpulumutsi wathu. Timakhulupilira kuti chifukwa cha imfa ya nsembe ya Yesu, anthu onse akhoza kulandira chikhulukiliro cha machimo ndi kukhalanso mu chiyanjano chabwino ndi Mulungu. Chifukwa chakuti tidayanjanitsidwa ndi Mulungu, timakhulupilira kuti tiyenera kuyanjanitsidwa wina ndi mnzake. Tikondane wina ndi mnzake monga momwe Mulungu adatikondera, ndi kukhululukirana wina ndi mnzake monga mmene Mulungu adatikhululukira. Timakhulupilira kuti Buku Lopatulika, buku loyera ndilo magwero a chowonadi chilichonse cha uzimu. Ife ndife agulu la chiyeretso la Wesley ndipo timavomereza mbiri ya chikulupiliro ndi zikhulupiliro za chikhristu.

2. NDIFE ANTHU ACHIYERETSO

Ndife anthu achiyeretso, oitanidwa mwa malemba ndipo okokedwa ndi chisomo kuti tipembedze Mulungu ndi kumukonda Iye ndi mtima wathu wonse, ndi moyo wathu wonse, ndi nzeru zathu zonse, ndi mphamvu zathu zonse, ndi kukonda anzathu monga momwe timadzikondera ifeyo. Timakhulupilira kuti ifeyo tikakhulupilira, Mzimu Woyera amayamba ntchito yotisanduliza, ndi kumatipatsa mphamvu tsiku ndi tsiku kuti tikhale anthu a chikondi ndi odzisunga mu uzimu, odzipatula ku chidetso, a chifundo ndi a chilungamo. Ndi ntchito ya Mzimu Woyera yomwe imatibwezeretsanso ife mu chifanizo cha Mulungu ndi kubala mwa ife chikhalidwe cha Khristu. Chiyeretso mu moyo wa anthu

okhulupilira chimadziwika bwino ndi mawu akuti “kufanana ndi Khristu”

3. NDIFE ANTHU OTUMIDWA

Ndife anthu a masomphenya opanga ophunzira ofanana ndi Yesu Khristu ku dziko lonse lapansi. Kutumidwaku kwayambira pa kusonkhana kwathu popembedza kenako ndi kumapita ku dziko lonse. Cholinga chathu ndi kuti tilandire okhulupilira atsopano mu chiyanjano cha oyera mtima ndi kuyamba ma gome ena atsopano opembedza.

Masomphenya athu ndi kuti tigawane ndi ena za chikondi cha Mulungu kwa onse ndi Chifundo chake kwa otayika/osochera ndi osweka mtima komanso kukumana ndi zosowa zenizeni za anthu opsinjidwa. Tili odzipereka kuitanira anthu ku chikhulupiliro, kusamalira iwo amene ali osowa ndi kuika anthu onse pamodzi amene adzaitana pa dzina la Ambuye.

Tili odzipereka ku ntchito ya kusula ndi kuphunzitsa ndi cholinga chakuti anthu, amuna ndi akazi akhale okonzeka ngati atsogoleri a chikhristu omwe adzatha kukwaniritsa ntchito yomwe Mulungu watiyitanira.

Mawu Oyamba

Buku ili ndi kalozera wakuti athandize mamembala ampingo kuti azindikire momwe mpingo wa Nazarene umayendetsedwera. Malumulo oyendetsera mpingo wa Nazarene ali mu buku lomwe limatchedwa kuti Buku La Malamulo Ndi Mayetsedwe A Mpingo Wa Nazarene (Manual). Buku La Malamulo Ndi Mayetsedwe A Mpingo Wa Nazarene ndi buku lamalamulo ndipo lidalembedwa mwatsatanetsatane. Koma anthu ambiri, makamaka amene chingerezi sichiyankhulo chobadwa nacho adachita kuphunzira, amavutika ndi chingerezi chomwe chidalembedwa mu Buku La Malamulo Ndi Mayetsedwe A Mpingo Wa Nazarene kotero kuti apeze tanthauzo la chomwe chikukambidwa zimavuta. Ichi ndi chifukwa chake buku ili lalembedwa mu mawu apafupi kufotokoza mfundo zikuluzikulu za pa mpingo ndi ku chigawo.

MASOMPHENYA A MPINGO WA NAZARENE (Manual p 62)

Nchito ya Mpingo wa Nazarene ndi kudziwitsa anthu onse za chisomo chotisintha cha Mulungu yemwe anatikhululukira ife machimo athu ndi kuyeretsa mitima yathu ndi mwazi wa Yesu Khristu. Masomphenya athu ndi kupanga ophunzira, kuwaika ophunzirawo mu chiyanjano ndi okhulupilira anzawo ndi kuti ankhale pa mpingo, kuwaphunzitsa ndi kuwalangiza momwe angatengere mbali pa kutumikira. Cholinga chathu ndi choti tiwone anthu atakhazikika mu moyo wa chiyero womwe ndi wokondweretsa Mulungu.

Ndi pa mpingo pomwe anthu amayenera kulimbikitsidwa ndi kukhazikika mu chikhulupiliro ndi kutumidwa kukachita ntchito.

Motero mpingo kapena kuti gome ndi lofunika zedi. Chifukwa cha dongosolo la kayendetsedwe ka mpingo, matchalitchi amaikidwa pagulu limodzi ndi kupanga chigawo, ndipo zigawo zimapanga ma Rijoni (Chigawo chachikulu)

NSANAMIRA ZA CHIKULUPILIRO ((1-22))

1. MULUNGU MMODZI MWA ATATU

Timakhulupilira mwa Mulungu mmodzi amene ndi wamuyaya, alibe malire ndipo kuti ndi Mulengi ndi wolamulira dziko lonse kumwamba ndi pansi. Mulungu ndi woyera mu chikhalidwe chake chonse ndipo adawonekera kwa ife monga Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera.

(Genesis 1; Levitiko 19.2; Deuteronomo 6:4-5; Yesaya 5:16, 6:1-7; 40:18-31; Mateyu 3:16-17; 28:19-20; Yohane 14:6-27; 1 Akorinto 8:6; 2 Akorinto 13:14; Agalatiya 4:4-6; Aefeso 2:13-18)

2. YESU KHRISTU

Timakhulupilira mwa Yesu Khristu, munthu wachiwiri pa utatu woyera, yemwe adali ndi Mulungu nthawi zonse, koma adakhala munthu ndipo adabadwa mwa Namwali Mariya. Yesu si munthu amene adachita kusanduka Mulungu, kapena kuti ndi Mulungu amene adachita mongokhala thupi la munthu ayi. Koma

Iyeyo ndi Mulungu ndithu ndi munthu wathuthu, ali ndi makhalidwe onsewa kupanga chimodzi.

Timakhulupilira kuti Yesu Khristu adayenda moyo wopanda uchimo ndi pang'ono pomwe, adayenda moyo wangwiro, wakumvera, adafa imfa ya nsembe ndipo mwa imfa yakeyo adagonjetsa mphamvu zonse za uchimo. Kudzera mu mphamvu ya Mulungu, adawuka kwa akufa ndipo monga Mwana wangwiro wa Mulungu (Mwana wa munthu adakwera kumwanba komwe akutipembedzera).

(Mateyu 1:20-25; 16:15-16; Luka 1:26-35; Yohane 1:1-18; Machitidwe 2:22-36; Aroma 8:3, 32-34; Agalatiya 4:4-5; Afilipi 2:5-11; Akolose 1:12-22; 2:15; 1 Timoteo 6:14-16; Ahebri 1:1-5; 7:22-28; 9:24-28; 1 Yohane 1:1-3; 4:23,15)

3. MZIMU WOYERA

Timakhulupilira mwa Mzimu Woyera yemwe ali munthu wachitatu mu Utatu Woyera, amalitsimikizira dziko lapansi za tchimo, amapereka moyo watsopano kwa onse amene alapa ndi kukhulupilira mwa Yesu, amatsogolera, kuphunzitsa ndi kuyeretsa okhulupilira.

(Yohane 7:39; 14:15-18, 26; 16:7-15; Machitidwe 2:33; 15:8-9; Aroma 8:1-27; Agalatiya 3:1-14; 4:6 Aefeso 3:14-21; 1 Atesalonika 4:7-8; 2 Atesalonika 2:13; 1 Petro 1:2; 1 Yohane 3:24; 4:13)

4. MALEMBA OYERA

Timakhulupilira kuti mabuku 66 a m'Buku Lopatulika ndi Mawu owuzilidwa ndi Mulungu. Timakhulupilira kuti Buku Lopatulika limatisonyeza ife china chili chonse chofunikira pa chipulumutso chathu.

(Luka 24:44-47; Yohane 10:35; 1 Akorinto 15:3-4; 2 Timoteo 3:15-17; 1 Petro 1:10-12; 2 Petro 1:20-21)

5. TCHIMO, LOBADWA NALO NDI LOCHITA WEKHA

Timakhulupilira kuti uchimo udadza mdziko lapansi chifukwa cha kusamvera kwa Adamu ndi Hava. Tchimo limeneli lidabweretsa imfa ndipo lidalekanitsa munthu ndi Mulungu.

Timakhulupilira kuti uchimo ulipo magulu awiri, uchimo umene munthu aliyense amabadwa nawo womwe ndi wotsutsana ndi chikhalidwe cha Mulungu, ndipo gulu lachiwiri la uchimo ndi zinthu zonse zoipa zimene anthu amachita.

5.1 Timakhulupilira kuti chifukwa cha kuchimwa kwa Adamu, anthu onse amabadwa ndi chikhalidwe cha uchimo. Chikhalidwe cha uchimochi chimatsutsana ndi Mulungu ndipo chimakakamiza anthu kuchita zoipa. Timakhulupilira kuti chikhalidwe cha uchimochi chimakhalabe mu mtima mwa mkhristu kufikira kuti chikachita kuchotsedwa ndi ntchito ya chiyeretso ya Mzimu Woyera.

5.2 Chikhalidwe cha uchimochi ndi chosiyana ndi ntchito za uchimo mwa njira yakuti chikhalidwe cha uchimo ndi chikhumbokhumbo cha mkati chomwe chimakakamiza anthu kuti achimwe. Anthu sawerengedwa uchimo pa chimenechi pokhapokha atanyozera kapena kukana chipulumutso cha Mulungu chomwe apatsidwa.

5.3 Tchimo ndi kuphwanya mwa dala lamulo lodziwika la Mulungu. Tchimo ndi losiyana ndi kulakwitsa, kuyiwala kapena kulephera kwina kuli konse komwe ndi zotsatira chabe za kuchimwa kwa munthu. Maganizo ndi machitidwe otsutsana ndi Mzimu wa Khristu amatchedwa kuti machimo ochimwira Mzimu. Tchimo ndi kuphwanya lamulo la chikondi ndi kusakhulupilira ntchito ya chipulumutso ya Ambuye Yesu.
(Tchimo lobadwa nalo - Genesis 3:6-5; Yobu 15:14; Masalimo 51:5; Yeremiya 17:9-10; Marko 7:21-23; Aroma 1:18-25; 5:12-14; 7:1-8:9; 1 Akorinto 3:1-4; Agalatia 5:16-25; 1 Yohane 1:7-8

Tchimo lochita yekha munthu; Mateyu 22:36-40 {ndi 1 Yohane 3:4}; Yohane 8:34-36; 16:8-9; Aroma 3:23; 6:15-23; 8:18-24; 14:23; 1 Yohane 1:9-2:4; 3:7-10)

6. CHIWOMBOLO

Timakhulupilira kuti Yesu Khristu adanzunzika; nakhetsa mwazi wake ndi kufa pa mtanda kuti atiwombole ku uchimo wathu ndi kutibwezeretsa mu chiyanjano ndi Mulungu. Timakhulupilira kuti palibe njira inanso yoti anthu apulumuke nayo, ndipo kuti Yesu adafera anthu onse. Yesu amapereka chipulumutso kwa ana ang'ono ndi onse omwe sangathe kupanga chiganizo pa wokha kamba ka zifukwa zina. Koma anthu ena onse (omwe si ana ang'ono kapena osatha kuganiza bwino pa wokha) ayenera kulapa ndi kukhulupilira Yesu pa wokha kuti apulumuke.

(Yesaya 53:5-6, 11; Marko 10:45; Luka 24:46-48; Yohane 1:29; 3:14-17; Machitidwe 4:10-12; Aroma 3:21-26; 4:17-25; 5:6-21; 1 Akorinto 6:20; 2 Akorinto 5:14-21; Agalatiya 1:3-4; 3:13-14; Akolose 1:19-23; 1 Timoteo 2:3-6; Tito 2:11-14; Ahebri 2:9; 9:11-14; 13:12, 1 Petro 1:18-21 2:19-25; 1 Yohane 2:1-2)

7. CHISOMO CHOKONZEDWERATU/CHOYIKIDWIRATU

Timakhulupilira kuti anthu adalengedwa mu chifanizo cha Mulungu kotero kuti ali ndi kuthekera kosankha pakati pa chabwino ndi choipa. Adamu adachimwa ndipo chifukwa cha kuchimwa kwa Adamu munthu aliyense amabadwa ndi chikhalidwe cha uchimo, ndipo kuti anthu sangathe kudzipulumutsa wokha ndi ntchito zawo zabwino zomwe angachite.

Timakhulupilira kuti chisomo cha Mulungu ndi chaulele ndipo kuti chidaperekedwa kwa anthu onse. Chisomo cha Mulungu chimapangitsa kuti munthu wina aliyense akhonza kusiya zoipa ndi kuyenda mu chilungamo, ndi kukhulupilira pa Yesu kuti apeze chikhululukiro cha uchimo ndi kusambitsidwa ku uchimo ngati atakhala ndi mtima wofuna kulapa.

Timakhulupilira kuti ngakhale kuti munthu wapulumutsidwa ndi kuyeretsedwa akhonza kugwa mu uchimo ndi kupita ndithu ku chiwonongeko ngati atapanda kulapa tchimolo.

(Chikhalidwe cha Mulungu ndi uchimo wa umunthu: Genesis 1:26-27, 2:16-17; Deuteronomo 28:1-2; 30:19; Yoswa 24:15; Masalimo

8:3-5; Yesaya 1:8-10; Yeremiya 31:29-30; Ezekieli 18:1-4; Mika 6:8; Aroma 1:19-20; 2:1-16; 14:7-12; Agalatiya 6"7-8)

(Kuperewera kwathu - Yobu 14:4; 15:14; Masalimo 14:1-4; 51:5; Yohane 3:6a; Aroma 3:10-12; 5:12-14; 20a; 7:14-25

Chisomo chaulere ndi ntchito za chikhulupiliro: Ezekiel 18:25-26; Yohane 1:12-13; 3:6b; Machitidwe 5:31; Aroma 5:6-8; 18; 6:15-16; 23; 10:6-8; 11:22; 1 Akorinto 2:9-14; 10:1-12; 2 Akorinto 5:18-19; Agalatiya 5:6; Aefeso 2:8-10; Afilipi 2:12-13; Akolose 1:21-23; 2 Timoteo 4:10a; Tito 2:11-14; Ahebri 2:1-3 : 3:12-15:6:4-6: 10:26-31: Yakobo 2:18-22: 2 Petro 1:10-11:2:20-22)

8. KULAPA

Timakhulupilira kuti anthu onse adachimwa ndipo adasiyanitsidwa kutali ndi Mulungu. Timakhulupilira kuti Mzimu Woyera amagwira ntchito mu miyoyo ya onse omwe amatembenuka ku uchimo ndi kulapa mowona mtima ndi kukhulupilira Khristu, adzalandira chikhululukiro cha machimo awo ndi kupeza moyo wosatha.

(2 Mbiri 7:14; Masalimo 32:5-6; 51:1-17; Yesaya 55:6-7; Yeremiya 3:12-14; Ezekieli 18:30-32; 33:114-16; Marko 1:14-15; Luka 3:1-14; 13:1-5; 18:9-14; Machitidwe 2:38; 3:19; 5:31; 17:30-31; 26:16-18; Aroma 2:4; 2 Akorinto 7:8-11; 1 Atesalonika 1:9; 2 Petro 3:9)

9. KULUNGAMITSIDWA, KUKONZEDWANSO NDI UMWANA

Timakhulupilira kuti onse okhulupilira mwa Yesu Khristu ndi kumulandira Iye ngati Mbuye ndi mpulumutsi amalungamitsidwa. Izi zikutanthauza kuti Mulungu amakhululukira machimo onse womwe adawachita, ndi kuwamasula ku chilango cha uchimo ndipo amawalandira ngati olungama.

Munthu akamulandira Yesu ngati mpulumutsi wake, munthu ameneyo wabadwa kwatsopano, ndipo amapatsidwa chikhalidwe china chatsopano. Moyo watsopano wauzimuwu, umakhala wachikhulupiliro, wachikondi, ndi wokondweretsa Mulungu.

Timakhulupilira kuti Mulungu mwa chifundo chake si kuti amangotikhululukira ndi kutipatsa moyo wa uzimu watsopano chabe

ayi, koma amatilandira mbanja lake ndi kutisandutsa ana ake. Zinthu zitatu izi; chikhululukiro, kubadwa kwatsopano ndi umwana, zonse zimachitika nthawi imodzi ndipo zimadalira pa kulapa kwathu ndi chikhulupiliro chathu mwa Khristu. Mzimu Woyera amachitira umboni kwa mzimu wathu ndi kutitsimikizira kuti Mulungu watipulumutsa.

(Luka 18:14; Yohane 1:12;-13; 3:3-8; 5-24; Machitidwe 13:39; Aroma 1:17; 3:21-26,28; 4:5-9, 17-25; 5:1, 16-19; 6:4; 7:6: 8:1, 15-17: 1Akorinto 1:30; 6:11; 2 Akorinto 5:17-21; Agalatiya 2:16-21; 3:1-14, 26; 4:4-7; Aefeso 1:6-7; 2:1, 4-5 Afilipi 3:3-9; Akolose 2:13; Tito 3:4-7; 1 Petro 1:23; 1 Yohane 1:9; 4:7; 5:1, 9-13,18)

10. CHIYERETSO CHANTHUTHU

Timakhulupilira kuti munthu utatha kubadwa mwatsopano, pali ntchito ina ya Mulungu momwe wokhulupilira amadzikhuthula kwa Mulungu kwathuthu, ndipo amamasulidwa ku tchimo lobadwa nalo. Izi zinathandiza wokhulupilirayo kuti akhale moyo wakumvera ndi chikondi kwa Mulungu ndi anthu.

Tikayeretsedwa, mwazi wa Yesu umatsuka mitima yathu, ndipo Mzimu Woyera amadzadza mitima yathu, kutipatsa mphamvu zotumikira Mulungu ndi kukhala moyo wa umulungu Mzimu Woyera amachita umboni kwa mzimu wathu kuti watitsuka ndi kutidzadza.

Chiyeretso chimatheka kudzera mu imfa ya Yesu Khristu. Udindo wa munthu pa chiyeretso ndi kuti adzipatula ku chidetso chili chonse ndi kukhulupilira Mulungu kuti wamuyeretsa. Ntchito imeneyi imadziwikanso ndi mawu akuti, “Chikondi cha ngwiro”, “chiyero cha mtima”, “Ubatizo wa Mzimu Woyera”ndi “chiyeretso cha chikhristu”.

Timakhulupilira kuti pali kusiyana kwakukulu pakati pa mtima woyera ndi kukhwima mu uzimu. Mulungu akhoza kuyeretsa mitima yathu nthawi imodzi koma kuti munthu akhale wokhwima mu uzimu ndi ntchito yomwe imachitika pang’ono pang’ono akamakula mu uzimu.

Timakhulupilira kuti munthu woyeretsedwa amakhala ndi chilakolako choti akule mu chisomo. Kukula kumeneku si kumangochitika pa kokhakokha ayi koma pamafunika chisamaliro chabwino cha uzimu kuti munthuyo akhale wofanana ndi Yesu mu

khalidwe ndi umunthu wake. Munthu amene sasamalira moyo wake wauzimu kuti ukule adzawononga umboni wake ndipo chisomo chomwe adachilandira mu moyo wake chikhoza kupsinjidwa kapena kutaika kumene.

(Yeremiya 31:31-34; Ezekieli 36:25-27; Malaki 3:2-3; Mateyu 3:11-12; Luka 3:16-17, 2 Akrorinto 6:14-7:1; Agalatiya 2:20; 5:26-25; Aefeso 3:14-21; 5:17-18, 25-27; Afilipi 3:10-15; Akolose 3:1-17; Ahebri 4:9-11; 10:10-17; 12:1-2; 13:12; 1 Yohane 1:7,9)

("Chikondi changwiro": Deuteronomo 30:6; Mateyu 5:43-48; 22:37-40; Aroma12:9-21; 13:8-10; 1 Akorinto 13; Ahebri 6:1; 1 Yohane 4:17-18)

"Ubatizo wa Mzima Woyera" Yeremiya 31:31-34; Ezikieli 36:25-27; Malaki 3:2-3; Mateyu 3:11-12; Machitidwe 1:5; 2:1-4; 15:8-9)

11. MPINGO

Mpingo umapangidwa ndi anthu onse omwe avomereza Yesu kukhala Mbuye wawo. Alowa mu pangano la ubwenzi ndi Mulungu kudzera mu kubadwanso Mwatsopano ndipo akhala gawo limodzi la thupi la Khristu. Mpingo umawonetsera moyo wake mu kukhala pamodzi mu kulambira, kulalika za Mawu a Mulungu, kuchita nawo ma sakaramenti, kumvera Khristu ndi kulimbikitsana wina ndi mnzake mu moyo wachikhristu.

Mpingo uli ndi udindo wopitiriza ntchito ya Ambuye Yesu Khristu mdziko lapansi kudzera mu moyo wachiyero, kufalitsa uthenga, kuphunzitsa ophunzira ndi kutumikira mwa mwachitidwe. Zinthu zonsezi zimachitika ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

Mpingo uli mu magulu awiri, mpingo wa pawokha kapena kuti tchalitchi ndi mpingo wa dziko lonse monga thupi la Khristu, ndipo umawonetsera moyo wake mu njira zosiyanasiyana mwa anthu a makhalidwe ndi miyambo yosiyanasiyana. Mpingo umawonetsetsa kuti Mulungu akuitana anthu ena ku mautumiki ena apadera ndipo mpingowo umawalimbikitsa anthu oterowo kuti alowe mu utumiki wa kufalitsa uthenga ndi utumiki wa chikondi. Mpingo umakhala pansi pa utsogoleri wa Mulungu ndi kumadikira kubweranso kwa chimwemwe kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

(Eksodo 19:3; Yeremiya 31:33; Mateyu 8:11; 10:7; 16:13-19; 24; 18:15-20; 28:19-20; Yohane 17:14-26; 20:21-23; Machitidwe 1:7-8; 2:32-47; 6:1-2; 13:1; 14:23; Aroma 2:28-29; 4:16; 10:9-15; 11:13-32; 12:1-8; 15:1-3;
1 Akorinto 3:5-9; 7:17; 11:-, 17-33; 12:3, 14:26-40; 2 Akorinto 5:11-6:1; Agalatiya 5:6, 13-14; 6:1-5, 15; Aefeso 4:1-17; 5:25-27
Afilipi 2:1-16; 1 Atesalonika 4:1-12; 1 Timoteo 4:13; Ahebri 10:19-25; 1 Petro 1:1-2, 13:2:4-12, 10-11; 1 Yohane 4:17; Yuda 24; chivumbulutso 5:9-10)

12. UBATIZO

Timakhulupilira kuti ubatizo ndi sakaramenti limene adakhazikitsa Ambuye Yesu Khristu. Ubatizo umawonetsera chikulupiliro cha munthu mu imfa ndi kuwuka kwa Yesu Khristu ndi chikhumbokhumbo cha munthu kuti atsate Yesu mu kumvera ndi mu chilungamo.

Chifukwa chakuti ubatizo ndi chizindikiro cha pangano latsopano, pakati pa munthu ndi Mulungu, ana ang'ono ayenera kubatizidwa ngati pempho la makolo ngati adzalonjeze kuwaphuniztsa anawo kukhala moyo wa chikhristu.

Anthu ayenera kubatizidwa pa kumuwaza madzi, pa kumuthira madzi kapena kumuviika m'madzi, kutengera kusankha kwa obatizidwayo.

(Mateyu 3:1-7; 28:16-20; Machitidwe 2:37-41; 8:35-39; 10:44-48; 19:1-6; Aroma 6:3-4; Agalatiya 3:26-28; Akolose 2:12; 1 Petro 3:18-22)

13. MGONERO WA AMBUYE

Timakhulupilira kuti mgonero udaikidwa ndi Yesu. Ndi chikumbukiro cha nsembe ya imfa ya Yesu ndipo kuti umabweretsa moyo ndi madalitso kwa iwo amene amadya mgonerowo mwa chikhulupiliro. Mgonero ndi wa onse amene ali ndi chikhulupiliro kuti kudzera mu imfa yake adalandira moyo ndi chipulumutso. Kudya mgonero kumatikumbutsanso kuti Yesu adzabweranso.

Okhawo amene ali ndi chikhulupiliro mwa Yesu, iwo amene anamukhulupilira Yesu, ndipo amakondana ndi okhulupilira anzawo ndi amene ali oyenera kudya mgonero.

(Eksodo 12:1-14; Mateyo 26:26-29; Marko 14:22-25; Luka 22:17-20; Yohane 6:28-58; 1 Akorinto 10:14-21; 11:23-32)

14. MACHILITSO

Timakhulupilira kuti Mulungu amachilitsa anthu odwala akapemphereredwa ndi anthu a Mulungu ndipo timalimbikitsa anthu kuti azipempherera anthu odwala ndi chikhulupiliro kuti achilitsidwe - Timakhulupiliranso kuti Mulugu amachilitsa kudzera mwa anthu a chipatala, anthu a sayansi koma osati a sing'anga azitsamba kapena a mizimu ayi.

(2 Mafumu 5:1-19; Masalimo 103:1-5; Mateyu 4:23-24; 9:18-35; Yohane 4:46-54; Machitidwe 5:12-16; 9:32-42; 14:18-15; 1 Akorinto 12:4-11; 2 Akorinto 2:7-10 Yakobo 5:13-16)

15. KUBWERANSO (KWACHIWIRI) KWA YESU

Timakhulupilira kuti Ambuye Yesu adzabweranso. Okhulupilira onse amene adzakhalebe ali ndi moyo sadzapitilira iwo akugona m'manda. Adzayamba kuwuka ndi okhulupilira akugona m'manda ndi kukakumana ndi Ambuye mlengalenga, ndipo tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse.

(Mateyu 25:31-46; Yohane 14:1-3; Machitidwe 1:9-11; Afilipi 3:20-21; 1 Atesalonika 4:13-18; Tito 2:11-14; Ahebri 9:26-28; 2 Petro 3:3-15; Chivumbulutso 1:7-8; 22:7-20)

16. KUWUKA, CHIWERUZO NDI CHITSIRIZO

Timakhulupilira kuti matupi a anthu olungama pamodzi ndi osalungama omwe adzawuka kwa akufa ndi kukalumikizidwa chomwe munthu aliyense adzaima pa maso pa Mulungu kuti aweruzidwe monga mwa ntchito zake zomwe adachita ali ndi moyo.

Timakhulupilira kuti onse omwe adakana kulapa ndi kukhulupilira mwa Khristu adzazunzika kwamuyaya mu gehena. Timakhulupiliranso kuti moyo wa ulemerero ndi wosatha ulipo kwa onse amene akhulupilira mwa Yesu, ndipo akumumvera ndi kumutsata mokhulupirika, Ambuye wathu Yesu Khristu.

(Genesis 18:25; 1 Samueli 2:10; Masalimo 50:6; Yesaya 26:19; Danieli 12:2-3; Mateyu 25:31-46; Marko 9:43-48; Luka 16:19-31; 20:27-38; Yohane 3:16-18; 5:25-29; Machitidwe 17:30-31; Aroma 2:1-16; 14:7-12; 1 Akorinto 15:12-58; 2 Akorinto 5:10; 2 Atesalonika 1:5-10; Chivumbulutso 20:11-15; 22:1-15)

MALAMULO KWA MAMEMBALA A MPINGO

Anthu omwe alandira Yesu monga mpulumutsi wawo, ndipo akufuna kulowa Mpingo wa Nazarene, ayenera kukhala moyo wa Umulungu. Mawu a Mulungu amatilangiza momwe tiyenera kukhalira.

MAMEMBALA A MPINGO AYENERA KUCHITA ZINTHU IZI: ((27.1))

1. Kukonda Mulungu ndi mtima wathu wonse, nzeru zathu, moyo wathu ndi mphamvu zathu zonse, ndi kukonda anzathu monga ife tomwe (Eksodo 20:3-6; Levitiko 19:17-18; Deuteronomo 5:7-10; Marko 12:28-31 Aroma 13:8-10).

2. Kugawana uthenga ndi ena omwe sanapulumuke, ndi kuwaitanira ku tchalitchi, ndi kuyesetsa kuwatsogolera kwa Khristu. (Mateyu 28:19-20; Machitidwe 1:8; Aroma 1:1416; 2 Akorinto 5:18-20).

3. Kuchitira ulemu kwa anthu onse (Aefeso 4:32; Tito 3:2; 1 Petro 2:17; 1 Yohane 3:18).

4. Kukhala wothandiza, wokoma mtima, wodekha ndi wokhululukira akhristu anzake. (Aroma 12:13; Agalatiya 6:2; 10; Akolose 3:12-14).

5. Kufunafuna kuchitira zabwino anjala, odwala, amndende, ndi osowa (Mateyu 25:35-36; 2 Akorinto 9:8-10; Agalatiya 2:10; Yakobo 2:15-16; 1 Yohane 3:17-18).

6. Kupereka zopereka ndi chachikhumi kuti zithandize ntchito ya mpingo (Malaki 3:8-10; Luka 6:38, 1 Akorinto 9:14; 16:1-2; 2 Akorinto 9:6-10 Afilipi 4:15-19).

7. Kusonkhana ndi ena ku tchalitchi mokhulupirika (Ahebri 10:25; Machitidwe 2:42), kudya mgonero (1 Akorinto 11:23-30), ndi kuchita mapemphero munthu payekha ndi kunyumba ngati banja (Machitidwe 17:11; 2 Timoteo 2:15; 3:14-16; Deuteronomo 6:6-7 Mateyu 6:6).

MAMEMBALA A MPINGO AYENERA KUPEWA ZINTHU IZI: ((27.2):)

1. Kutchula dzina la Yehova pachabe (Eksodo 2:7; Levitiko 19:12; Yakobo 5:12).

2. Kuchita ntchito zolemetsa pa tsiku la sabata ndi kulipeputsa ngati tsiku losapatulika (Eksodo 20:8-11; Yesaya 58:13-14; Marko 2:27;-28; Machitidwe 20:7; Chivumbulutso 1:10).

3. Chiwerewere cha mtundu uli wonse (Eksodo 20:14; Mateyu 5:27:32; 1 Akorinto 6:9-11; Agalatiya 5:19 1 Atesalonika 4:3-7).

4. Zizolowezi kapena makhalidwe omwe akhonza kuwononga matupi athu kapena ubongo wathu. Tizikumbukira kuti ndife akachisi a Mzimu Woyera (Miyambo 20:1; 231-3; 1 Akorinto 6:17:20; 2 Akorinto 7:1; Aefeso 5:18)

5. Kukangana, miseche, ndi kuwanditsa nkhani zomwe zikhoza kuwononga mbiri yabwino ya anthu ena (2 Akorinto 12:20; Agalatiya 5:15; Aefeso 4:30-32; Yakobo 3:5-18; 1 Petro 3:9-10).

6. Kusakhulupirika, chinyengo mu malonda, kunena mabodza (Levitiko 19:10-11; Aroma 12:17; 1 Akorinto 6:7-10).

7. Makhalidwe ndi kuvala monyada. Anthu ayenera kuvala modzichepetsa ndi mwa ulemu kuti awonetsere moyo wa kuyera mtima (Miyambo 29:23; 1 Timoteyo 2:8-10; Yakobo 4:6; 1 Petro 3:3-4; 1 Yohane 2:15-17).

8. Nyimbo, mabuku ndi zisangalalo zimene sizilemekeza Mulungu (1 Akorinto 10:31; 2 Akorinto 6:14-17; Yakobo 4:4).

NTHAWI ZONSE TAYENERA:

Kukhala mu chiyanjano changwiro ndi mpingo. Osawukira atsogoleri a mpingo, koma kukhala wodzipereka ku ziphunzitso ndi malamulo a mpingo, ndi kukhala wochitachita mu utumiki wa kufalitsa uthenga (Aefeso 2:18-22; 4:1-3, 11-16; Afilipi 2:1-8; 1 Petro 2:9-10).

PANGANO LA MAKHALIDWE A CHIKHRISTU

Mutu uwu ndi chidule cha pangano la makhalidwe a moyo wa chikhristu wopezeka mu Buku La Malamulo Ndi Mayendetsedwe A Mpingo Wa Nazaren.

A. MOYO WA CHIKHRISTU

33. Mpingo umafalitsa uthenga wabwino mwa chimwemwe wakuti tikhoza kumasulidwa ku uchimo ndi kulowa m'moyo watsopano mwa Khristu. Ndi chisomo cha Mulungu ifeyo a Khristu sitiyenera kutsatanso makhalidwe a uchimo ndi ntchito zoipa zakale. Koma tiyenera kuvala, 'munthu watsopano' - njira yatsopano ndi yoyera ya moyo pamodzi ndi mtima wa Khristu (Aefeso 4 :17-24).

33.1. Mpingo wa Nazarene umayesetsa kuti mfundo za m'Buku Lopatulika zomwe zakhala zilipo kuchokera kalekale zigwirizane ndi nthawi yathu ino, mu njira yonera kuti ziphunzitso ndi malamulo a mpingo zikhale zodziwika ndi zomveka bwino pakati pa anthu a miyambo ndi makhalidwe. Timakhulupilira kuti malamulo khumi amayala maziko a makhalidwe a moyo wa chikhristu choncho ndi woyenera kutsatidwa.

33.2. Timakhulupiliranso kuti Mzimu Woyera amatsogolera mpingo kuti ukhale ndi chikumbu-mtima chofanana cha chikhristu. Mpingo wa Nazarene ngati mpingo wa maiko onse umafunafuna njira zakuti pakhale njira ya moyo wa chiyero. Pangano la moyo wa chikhristu ndi lofunika kuti litsatidwe ngati kalozera ndi thandizo ku moyo wachiyero. Anthu omwe satsatira izi amawononga moyo wakuchitira umboni wa mpingo ndi kufoketsa miyoyo yawo ya uzimu iwo eni.

33.3. Ndi zosatheka, ndipo ndi zosathandiza kuti tilembe tchimo la mtundu uli wonse lochitidwa m'dziko lapansi. Chofunika ndi chakuti mamembala onse a mpingo afunefune thandizo la Mzimu Woyera kuti athe kusiyanitsa chabwino ndi choipa. "Yesani zinthu zonse, sankhani chokomacho. Mupewe mawonekedwe onse a choipa." (1 Atesalonika 5:21-22)

Atsogoleri a mpingo azipereka chiphunzitso cha m'buku lopatulika chomwe chingathandize anthu kuti athe kusiyanitsa pakati pa chabwino ndi choipa.

33.4. Maphunziro ndi wofunika kwambiri ku moyo wakuthupi ndi wa uzimu womwe pakati pa wathu. Sukulu za boma ndi ena amangopereka maphunziro a dziko la pansi, chifukwa cha chimenechi ndi pofunika kuti mpingo kudzera mu maphunziro a Sande sukulu, ma koleji ndi ma seminale uziphunzitsa mfundo za m'Buku Lopatulika ndi makhalidwe abwino apamwamba.

33.5. Maphunziro a chiyero ndi ofunika kuti azichitikanso m'manyumba mwathu. Akhristu azilimbikitsidwa kukalowa ntchito m'sukulu za boma ndi zina ndi cholinga chakuti azikachitira umboni wa Yesu ndi kubweretsa kusintha komweko.

Makhalidwe awa ndi ofunika kuwapewa.

A. PEWANI ZISANGALALO ZOMWE ZIMATSUTSANA NDI CHIKHRISTU.

34. Akhristu ayenera kutsata mfundo zitatu zofunika kwambiri.

1. Kukhala mdindo wa chikhristu kumatanthauza kuti kumakhala ndi nthawi yopumula monga momwe tinakhalira ndi nthawi yogwira ntchito.
2. Akhristu adaitanidwa kukhala moyo wachiyero. Pali mabuku ambiri, wailesi , wailesi za kanema ndi zina za pa intaneti zimene zimabwera m'makomo athu. Tiyenera kupewa mabuku onse ndi mapologalamu ali wonse omwe akhonza kutichotsa pamaso pa Mulungu ndi pa moyo wa chiyero. Tizithandiza ndi kulimbikitsa zinthu zimene ndi zabwino ndi zothandiza.

3. Ngati akhristu tiyenera kudzudzula zinthu zimene zimakana Mulungu ndi kupititsa patsogolo uchimo, nkhanza ndi chiwerewere. Tizipewa chisangalalo chili chonse chomwe chimapangitsa kuti tchimo liwoneke ngati

chinthu chabwino ndi chokoma, ndi kuchepsa mlingo wa chiyero wa mtima ndi moyo womwe Mulungu adawuika.

Anthu athu aphunzitsidwe kugwiritsa ntchito chidziwitso cha mu pemphero ndi kusankha khwalala la moyo wa chiyero. Tizigwiritsa ntchito muyeso womwe John Wesley adapatsidwa "Chilichonse chimene chimachotsa kukoma kwa zinthu za uzimu mwa iwe, chili chonse chimene chimakulitsa ulamuliro wathupi pa malingaliro ako, chinthu choterocho mwa iwe ndi uchimo." (Aroma 14:7-13; 1 Akorinto 10:31-33; Aefeso 5:1-18; Afilipi 4:8-9; 1 Petro 1:13-17; 2 Petro 1:3-11)

34.2. Pewani zinthu monga kamayika munthu, kaliapa, pakati pa lamba ndi mtundu uliwonse wa njuga chifukwa choti zinthu izi zimawononga anthu ozichitawo ndi athu ena. (Mateyu 6:24-34; 2 Atesalonika 3:6-13; 1 Timoteyo 6:6-11; Ahebri 13:5-6 ; 1 Yohane 2:13-17).

34.3. Musalowe mabungwe amene amafuna kuti munthu alumbile mwa chinsinsi polowa. (1 Akorinto 1:26-31; 2 Akorinto 6:14-7:1; Aefeso 5:11-15; Yobu 4:4; 1 Yohane 2:15-17).

34.4. Pewani kuvina kuli konse kumene kukhonza ku tchinga kukula kwa moyo wauzimu ndi kuchotsa munthu ulemu wake. (Mateyu 22:36-39; Aroma 12:1-2; 1 Akorinto 10:31-33; Afilipi 1:9-11; Akolose 3:1-17).

34.5. Pewani kumwa kapena kugulitsa zakumwa zoledzeletsa. Kugulitsa kapena kugwiritsa ntchito fodya kapena mankhwala ozunguza bongo kapena chamba.

Buku Lopatulika komanso umunthu zimawonetsa kuti kumwa zakumwa zoledzeretsa ndi kusuta fodya kukhoza kudzetsa mavuto a kuthupi ambiri. Ndiye popeza kuti cholinga chathu ndi kuti tikhale moyo wa chiyero, tisagwiritse ntchito zinthu zimenezi. Buku Lopatulika limaphunzitsa kuti thupi lathuli ndi kachisi wa Mzimu Woyera, motero tikuwuza anthu athu kuti asakhundzane ndi zinthu izi, zoledzeretsa kapena zosokoneza ubongo. Nthawi zonse miyoyo yathu ikhale umboni ndi Buku Lopatulika limene anthu ena akhoza kuwerenga. (Miyambo 20:1; 23:29-24:2; Hoseya 4:10-11; Habakuku 2:5; Aroma 13:8; 14:15-21; 1 Akorinto 3:16-17; 6:9-12; 19:20; 10:31-33; Agalatiya 5:13-14,21; Aefeso 5:18).

34.6. Tisamwe mankhwala amphamvu kwambiri amene akhoza kusokoneza ubongo wa munthu kapena thupi lake, popanda malangizo

a dokotala. (Mateyu 22:37-39; 27:34; Aroma 12:1-2; 1 Akorinto 5:19-20; 9:24-27).

B. UKWATI NDI KUTHETSA UKWATI

35. Pali zinthu zambiri zimene zimachitika zofooketsa ndi kuwononga ukwati ndi banja la chikhristu. Ndi pofunika abusa azilalikira mosapsatira za dongosolo la Mulungu la ukwati kuti ndi malire imfa. Mipingo imafunika kuti ikhazikitse mapulogalamu amene angathandize kulimbitsa ndi kumanga mabanja a chikhristu.

Ukwati udaikidwa ndi Mulungu ndipo ndi mgwirizano wa umodzi wa mwamuna mmodzi ndi mkazi mmodzi mu chiyanjano, kuthandizana ndi kubereka ana. Anthu asalowe m'banja mothamanga ayi, koma ayambe apemphera kuti awone chitsogozo cha Mulungu. Pangano la ukwati ndi lomangika nthawi zonse ngati anthu awiriwo ali ndi moyo, ndipo kuthetsa ukwati ndi kuphwanya dongosolo la Mulungu la ukwati. (Genesis 1:26-28, 31; 2:21-24; Malaki 2:13-16; Mateyu 19:3-9; Yohane 2:1-11; Aefeso 5:21-6:4; 1 Atesalonika 4:3-8; Ahebri 13:4)

35.1. Buku Lopatulika limaphunzitsa kuti ukwati ndi kudzipereka kwa mwanuna ndi mkazi kwa wina ndi mzake malire imfa. Ukwati udaikidwa kuti ndi wosatha pokhapokha imfa motero kuti kuthetsa ukwati ndi zotsutsana ndi chiphunzitso cha Khristu.

Kuthetsa banja kapena kuti sikuti ndi tchimo lakuti Mulungu sangakhululuke ngati munthu atalapa mwa mtima, mwachikhulupiliro ndi modzichipetsa. Timadziwa kuti anthu ena amathetsa ukwati wawo kapena kuti amachotsedewa pa ukwati chifukwa cha malamulo adziko ndi pofuna chitetezo cha moyo wawo ku thupi.

(Genesis 2:21-24; Marko 10:2-12; Luka 7:36-50; Yohane 7:53-8:11; 1 Akorinto 6:9-11; 7:10-16; Aefeso 5:25-33)

35.2. Atumiki a Mulungu mu mpingo wa Nazarene aziphunzitsa anthu mu mpingo kupatulika kwa ukwati. Nthawi zonse azipereka uphungu kwa mnyamata ndi mtsikana womwe akufuna kuti akwatirane asadadalitse ukwati wawowo. Izi ziyenera kukhalanso choncho kwa anthu amene adasudzulidwa pa ukwati ndipo akufuna kuti akwatiwenso kapena kukwatiranso. Atumiki a Mulungu amange

ukwati wokhawo womwe ndi wovomerezeka kumangidwa molingana ndi Mawu a Mulungu.
Mamembala ampingo omwe mabanja awo akusowa mtendere ayesetse kupeza njira zothetsera mavutowo. Izi zichitike molingana ndi malonjezo amene adachita ndiponso motengera chiphunzitso cha Buku Lopatulika. Ayesetse kuteteza banja lawolo ndi kusachititsa manyazi dzina la Khristu Yesu - kapena mpingo wake. Anthu amene ali mmavuto akuluakulu a banja afunefune uphungu ndi malangizo kwa abusa awo ndi atsogoleri ena a uzimu.
35.4. Chifukwa cha kusadziwa, tchimo, ndi zofooka za munthu, anthu ambiri satsatira dongosolo la Mulungu. Timakhulupilira kuti Mulungu akhoza kuwapulumutsabe anthu amenewa monga momwe Yesu adathandizira mzimayi wa ku Samaria uja. Anthu amene adalekana ndi kubwererana, ayenera kufunafuna chisomo cha Mulungu kuti chiwathandize mu ukwati wawo. Anthu oterewa akhonza kulandilidwanso ngati mamembala mu mpingo ngati akuwonetsa kuti alapa ndipo adziwa kuyera kwa ukwati.

C. KUCHOTSA MIMBA

Mpingo wa Nazarene umakhulupilira kuti moyo wa munthu, ngakhale wa mwana amene asanabadwe ndi wopatulika ndipo umapatsidwa kwa ife ndi Mulungu. Sitiloledwa kuchotsa mimba mwa njira ina iliyonse. Timadziwa kuti pali nthawi zina kuti moyo wa mayi, kapena wa mwana wosabadwayo, kapena nthawi zina miyoyo yonse iwiri ili pa chiswe. Zikatero, kuchotsa mimbayo kuchitike ndi uphungu wa achipatala ndi uphungu wa Chikhristu.

Sitiloledwa kuchotsa mimba motero tayenera kukhala odzipereka ku mapulogalamu othandiza azimayi ndi ana. Ngati mayi wapeza kuti ali ndi pakati pamene samayembekezera, mpingo uthandize popereka chikondi, mapemphero, ndi uphungu. Izi zikhoza kuchitika kudzera mu kukhala ndi malo apadela a amayi oyembekezera komanso kukhala ndi mapulongalamu oti Akhristu azitha kutenga ana osowa thandizowo ndi kuwasandutsa ana awo.

Nthawi zambiri anthu amafuna kutaya mimba chifukwa chakuti sadatsatire malangizo a Chikhristu akugonana. Mpingo uli ndi

udindo wa kuphunzitsa anthu za kukhalira malo amodzi mwamuna ndi mkazi kuchokera m'malemba.

(Eksodo 20:13; 21:12-16; Yobu 31:15; Masalimo 22:9; 139:3-16; Yesaya 44:2; 24; 49:5; Luke 1:23-25, 36-45; Aroma 12:1-2; 1 Akorinto 6:16; 7:1; 1 Atesalonika 4:3-6)

D. KUGONANA

Kugonana ndi njira imodzi ya kuwonetsela chiyero ndi kukongola komwe Mulungu adakonza mu chilengedwe chake. Ndi imodzi mwanjira zimene pangano pakati pa mwamuna ndi mkazi limasindikizidwila ndi kuwonetseredwa. Ndi chinthu chodalitsidwa ndi Mulungu kwa anthu omwe ali mbanja ndipo kumawonetsera chikondi ndi kukhulupilirana.

Ana aphunzitsidwe kupatulidwa kwa chikhalidwe cha kugonana kochitika ndi anthu amene ali pa chikondi m'banja, modekha ndi kukhulupilirana mu mabanja a Chikhristu.

Atsogoleri ndi aphunzitsi mu mpingo azifotokoza chikhulupiliro cha Achikhristu pa nkhani ya kugonana. Aziwafotokozera Akhristu kuti aziwona kuti kugonana pakati pa anthu omwe akwatilana ndi kovomerezeka ndipo ndi chinthu chabwino ndi chodalitsidwa, ndi kupewa zinthu zimene zingapangitse kuti cholinga chake chipotozedwe kapena kuwonongedwa.

Mtundu uli wonse wa kugonana wochitika kunja kwa ukwati pakati pa mwamuna ndi mkazi woti Sali pa banja, ndi kotsutsana ndi Mawu a Mulungu.

Kugonana kwa amuna okhaokha ndi imodzi mwa njira zimene zimawononga cholinga cha kugonana. Timagwirizana ndi momwe limanenera Buku Lopatulika kuti machitidwe oterewa ndi uchimo ndipo akudikila mkwiyo wa Mulungu. Timakhulupilira kuti chisomo cha Mulungu ndi chokwanila kugonjetsa mchitidwe wa kugonana amuna okhaokha. (1 Akorinto 6:9-11). (Genesis 1:27; 19:1-25; Levitiko 20:13; Aroma 1:26-27; 1 Timoteo 1:8-10)

E. UDINDO WA MKHRISTU

38. Tanthauzo la Udindo. Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti Mulungu ndiye mwini wake wa anthu ndi zinthu zonse. Ndife adindo ake akusamalira ndi kugwiritsa ntchito moyenera moyo wathu ndi zomwe tili nazo. Tsiku lina lilipo lomwe Mulungu adzatifunsa za udindo womwe Iye adatipatsa. Mulungu adakhazikitsa ndondomeko ya kupereka chachikhumi chimene chimatanthauza kuperekeka chinthu chimodzi pa zinthu khumi zomwe tapeza, kwa Mulungu ndi udindo wathu. Izi zimaonetsa umwini wa Mulungu ndi udindo wathu.
(Malaki 3:8-10; Mateyu 6:24-34; 25:31-46; Marko 10:17-31; Yohane 15:1-17; 1 Akorinto 9:7-14; 2 Akorinto 6:1-15; 9:6-15; 1 Timoteyo 6:5-19; Ahebri 7:8; Yakobo 1:27; 1 Yohane 3:16-18)

38.1. Chakhumi cha ku Nyumba Yosunguramo. Kupereka chachikhumi cha kunyumba yosungiramo ndi njira imene Buku Lopatulika lidapereka kuti mamembala a mpingo apereke mokhulupilika ndi mosadukiza ku mpingo kwawo. Mamembala onse a mpingo wa Nazarene amapemphedwa kuti apereke limodzilimodzi la zomwe apeza ku mpingo womwe iwo amapemphera mokhulupilika. Chopereka cha ufulu ndi chopereka chowonjezera, pamwamba pa chopereka chakhumi, kuti chithandize mpingo wonse, ku distilikiti (chigawo), rijon, ndi ku likulu la mpingo.

Mipingo imapemphedwa kupereka mabajeti awo ku distilikiti, ku rijoni ndi ku likulu la mpingo pa mwezi uliwonse.

38.3. Kuthandiza Utumiki. "Ambuye adalamulira kuti iwo akulalikira uthenga akhale ndi moyo pakulalikira uthengawo" (wa mkachisi adye za….1 Akorinto 9:14). Mpingo wayenera kuthandiza atumiki ake omwe adaitanidwa ndi Mulungu ndipo amadzipereka ku ntchito ya utumiki. Kuti izi zitheke mamembala ampingo ayenera kumapereka chachikhumi chawo mowilikiza, ndi kulipila abusa awo mwezi uliwonse.

38.4. Chuma Chosiyidwa ndi Kulemba Wilu. Akhristu akhale okhulupilika kupereka chakhumi ndi zopereka akadali ndi moyo.

Azikonzeratunso chomwe adzachite ndi ndalama zawo ndi katundu wawo amene adzakhale iwo atamwalira. Motero Akhristu azilemba wilu atapemphelera ndiponso aziganizira kuthandiza ntchito ya mpingo ndi chuma chawo chosiyidwa.

F. Maudindo Ampingo

Mpingo kapena mipingo izisankha anthu pa udindo okhawo amene akuwonetsa kuti adatembenukadi mtima ndipo amayenda mu moyo wa chiyero mwa chisomo cha Mulungu. Akhalenso kuti iwowo amatsatira chiphunzitso, malamulo ndi machitidwe a mpingo wa Nazarene, ndipo kuti amathandiza mpingo mokhulupilika, mu kubwera ku tchalitchi, kupereka chachikhumi ndi zopereka.

G. Malamulo a Dongosolo

Mpingo utsate ndondomeko yoyenera monga momwe alili malamulo a dongosolo a Robati pokhala ndi misonkhano ya pa tchalitchi, ya ku distilikiti ndi ku likulu.

H. Kukonzanso Pangano la khalidwe la Chikhristu

Pangano La Makhalidwe A Akhristu likhonza kuchotsedwa kapena kusinthidwa ngati mavoti ofuna kutelo akwana oposa theka la anthu ovota ku Msonkhano Wa Ukulu Wa Mpingo Wonse.

Mayendetsedwe A Mpingo

Pali njira zitatu za kayendetsedwe ka mpingo;

1. Mipingo ina ili ndi mphamvu zambiri kwa atsogoleri.
2. Pomwe mipingo ina mphamvu zili ndi wanthu. Palibe mdindo wina aliyense kapena munthu amene ali ndi mphamvu zambiri. M’malo mwake maudindo amagawidwa kwa akulu a mu mpingo.
3. Pomwe pali njira yina yomwe imakhala yakuti mphamvu ndi zogawana pakati pa anthu ndi atsogoleri kapena kuti likulu.

Kayendetsedwe ka mpingo kokhala ndi mphamvu kwa atsogoleri kamatchedwa mu chingesezi kuti EPISCOPAL FORM OF GOVERNMENT. Pomwe kayendetsedwe komwe ndi kokhala ndi mphamvu kwa anthu kanatchedwa kuti CONGREGATIONAL FORM OF GOVERNMENT.

Mpingo wa Nazarene umatsatira kayandetsedwe kokhala ndi mphamvu zogawana atsogoleri ndi anthu, (Representative form of government), pomwe mbusa ndi akomiti amagawana mphamvu pa zochitika za pa tchalitchi ndi kayendetsedwe ka tchalitchi.

Timakhulupilira kuti ndi zofunika kuti pazikhala ma DS (District Superintendent) othandiza mipingo kukwanilitsa masomphenya ndi zolinga zake. Ulamuliro wa DS, kapena kuti mtsogoleri wa chigawo, asamalowerere zochitika za pa tchalitchi yoyima payokha. Mpingo uli wonse ukufunika, kuyang'anira nkhani ya ndalama za pa tchalitchipo, ndi zinthu zina zokhudzana ndi patchalitchipo ndi ntchito zake.

Mapangidwe ndi Kayendetsedwe ka Mpingo wa Nazarene

Dokotala Phineas Breese, munthu amene adayanbitsa mpingo wa Nazarene, adali mtumiki wa Mulungu kwa nthawi yayitali mu mpingo wa Methodist. Iye adawona kuti mpingo unkasowa atsogoleri woti azilimbikitsa ndi kuyendela abusa. Koma sadafune kutenga dzina lakuti bishopu lotchulila atsogoleri a abusawo koma dzina lakuti ma "Superintendent" mukhoza kuwona kuti dzina lakuti Superintendent likuimira ngati mtsogoleri wa timu ya mpira kapena kochi amene amalimbikitsa ndi kuthandiza abusa pa disilikiti yake kapena kuti chigawo chake.

Ku mbali ya kummawa kwa dziko la America, kudali mipingo ina imene idali pa kalikiliki kulalikila za kufunika kwa akhristu kuti ayende moyo wa chiyero. Mipingo imeneyi inkawona kuti ma bishopu ankalowerela kwambiri ndi nkhani za pa tchalitchi. Choncho mipingo inatsindika pa mfundo yakuti pa tchalitchi pa zikhala komiti yomwe izikhala ndi mphamwu zoyang'anila kayendetsedwe ka tchalitchiyo.

Ndiye pamene magulu awa (a matchalitchiwa) adaganiza zakuti aphatikizane kuti apange mpingo wa Nazarene, adayesetsa kutolelatolela maganizo osiyanasiyana a utsogoleri wa mpingo. Pamapeto adamvana kuti azikhala ndi ma Superintendent osati ma bishopu kutsogolera matchalitchi. Adagwirizanaso kuti mipingo izikhala ndi mphamvu zosankha mbusa wawo ndi kuyang'anila zochitika zonse za pa tchalitchipo. Mbusa azigwilira ntchito limodzi ndi komiti ya pa tchalitchi poyendetsa mpingowo.

Ku disilikiti, disilikiti superintendenti amagwira ntchito limodzi ndi komiti ya disilikiti yotchedwa Disilikiti Adivaizale Komiti pa kutsogolera ndi kuyang'anila matchalitchi. Ku likulu la mpingo la dziko lonse lapansi, kumakhala ma Jenolo Superintendent omwe amagwira ntchito limodzi ndi komiti ya dziko lonse kutsogolera ndi kuyang'anira Mipingo.

Pali magawo atatu a kayendetsedwe ka mpingo mu tchalitchi ya Nazarene. Magawo ake ndi yawa:

1. Gawo loyamba - Pa Tchalitchi
2. Gawo lachiwiri - Msonkhano wa chigawo (distilikiti)
3. Gawo lachitatu - Masonkhano wa dziko lonse (Jenelo Asembule)

Ndi zofunikira kudziwa momwe gawo lililonse limagwilira ntchito kuti tidziwe mmene Mpingo wonse umayendetsedwela.

Mitu itatu ili kutsogoloku ikufutokoza mmene gawo lili lonse la magawo atatuwa limakhalira.

Mpingo wa Nazarene pa Tchalitchi

Gawo lofunika kwambiri la mpingo wa Nazarene ndi la pa tchalitchi chifukwa ndi kumene anthu amabwera kudzapembedza, anthu atsopano amatembenukilako mtima ndi kukhala akhristu ndi kukhala mu miyoyo yawo ya uzimu. Ndi kumene anthu amayambila mpingo.

Umembala wa Mpingo (107-110)

Pali zinthu zinayi zofunika kuti munthu akhale membala weniweni wa mpingo wa Nazarene:

1. Achitire umboni kuti adamulandila Yesu ngati mpulumutsi wawo.
2. Agwirizane ndi zikhulupiliro za mpingo wa Nazarene.
3. Alonjeze kuti adzatsatira malamulo a mpingo wa Nazarene.
4. Alonjeze kuti adzathandiza mpingo ndi nthawi yake; pa kubwera ku tchalitchi mokhulupilika, kutenga nawo mbali pa zochitika za pa tchalitchi ndi kuthandiza mpingo ndi ndalama.

Membala wa mpingo ndi wosiyana kwakukulu ndi munthu amene amangobwera kutchalitchi kudzapemphera. Membala wa mpingo ndi munthu amene adadzipereka pa gulu kuti akhala chiwalo cha mpingo ndipo kuti azipezeka mu zochitika za pa tchalitchi ndi kuthandiza ntchito yake.

M'mene Munthu Angakhalile Membala

1. Anthu omwe akufuna kukhala mamembala a mpingo adziwe kuti Yesu Khristu ndi mpulumutsi wawo.
2. Azibwera ku maphunziro amene amafotokoza za ziphuzitso za mpingo.
3. Azibwera ku maphunzilo amene amafotokoza za malamulo ampingo za mmene Akhristu ayenela kukhalira.
4. Bungwe la kufalitsa uthenga ndi komiti ya umembala ya mpingo azifunsa mafunso anthuwo. Akayankha mafunsowo moyenera, akhoza kulandilidwa kukhala mamembala ampingo ndi abusa pa nthawi ya mapemphero.

Zokambirana za pa Tchalitchi (113)

Zokambirana za pa tchalitchi ndi chinthu chofunikira cha pa tchalitchi pamene mamembala a mpingo amakumana kuti akambirane ndi kuwona zoti achite pa moyo, kukula ndi kayendetsedwe ka zinthu pa tchalitchipo.

Mbusa amakhala wa pa mpando wa zokambilanazo.

Mlembi wa komiti ya pa tchalitchi ndi amene amalembela zokambilanazo. Zokambilana za pa chaka za pa tchalitchi ziyenera kuchitika patangotsala miyezi iwiri msokhano wa pa chaka wa chigawo kuti uchitike.

Mipingo yambiri ili ndi gulu la chiyanjano la amayi ndi gulu la chiyanjano l'abambo ngati gawo limodzi la zochitika za pa tchalitchipo. Izi mulibe mu buku la malamulo ampingo wa Nazarene lotchedwa 'Manyo' koma taziphatikizamo mu buku lino chifukwa chakuti ndi gawonso lofunika mu mipingo yambiri.

Ntchito ya Msonkhano wa Zokambirana za pa Tchalitchi

Zokambilana za pa tchalitchi zimakhala ndi ntchito ziwiri:

1. Kumva ma lipoti
2. Kuchita masankho.

Malipotiwa amakhala ochokera kwa:

1. Mbusa (413.15)
2. Mtsogoleri wa NMI (153.2)
3. Mtsogoleri wa NYI 151.4)
4. Mtsogoleri wa gulu la mgwirizano wa amayi
5. Mtsogoleri wa gulu la chiyanjano la abambo
6. Amene adalandira chiphatso cha ulaliki (428.1)
7. Adindo (Stewards)
8. Asungi (Trustees)
9. Mlembi wa patchalitchi (135.2)
10. Msungi Chuma (136.5)
11. Mtsogoleri wa Sande Sukulu ndi Kuchitira Umboni (146.6)

Msonkhano wa zokambilanawu umafunika kuti usankhe anthu awa :

1. Adindo (Stewards) (137)
2. Asungi (Trustees) (141,142.1)
3. Sande Sukulu Superintendenti (146)
4. Komiti yowona za Sande Sukulu (145)
5. Mtsogoleri wa bungwe la amayi
6. Mtsogoleri wa bungwe la abambo

Ntchito ya Mbusa

Mbusa ndi munthu amene akutsogolera tchalitchi kapena amene adalandira chiphatso cha Mlaliki ku distilikiti.

Mbusa amachimva kuti Mulungu adamuitana kukalalika Mawu a Mulungu - ndi kukasamalira anthu a Mulungu. Mbusa ali ndi ntchito yambiri yoti azichita. Zonsezi zilipo mu Buku La Malamulo a Mpingo (412-420). Ntchito yonseyi ikhonza kuikidwa mu magulu atatu akulu akulu:

1. Kulalikira ndi Kukonza Mapemphero

- Kulalikila
- Kubatiza, kudyetsa mgonero, kumanga ukwati ndi kuikitsa maliro
- Kukonza ma pulogalamu a kufalitsa uthenga pa tchalitchi.

2. Kuyang'anira Mamembala a Mpingo

- Kuyendera akhristu.
- Kusamalira odwala ndi osauka
- Kutonthoza olira.
- Kulimbikitsa Akhristu pa moyo wawo wauzimu.
- Kuthandiza anthu otaika kuti atembenuke ndi kubwera kwa Mulungu.
- Kuthandiza Akhristu kuti adzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi kukhala moyo wa chiyero.
- Kuphunzitsa ndi kulimbikitsa Akhristu mu chikhulupiliro chawo mwa Mulungu.

3. Kukonza Mapulogalamu a pa Tchalitchi

- Kulandira anthu kukhala mamembala.
- Kuyang'anila mabungwe a patchalitchi. (NYI, NMI, Sande Sukulu, Amayi a Chigwirizano, Chiyanjano cha Abambo ndi ena)

- Kupereka lipoti la pa chaka ku mpingo ndi kukapereka lipoti ku msonkhano wa pachaka wa distilikiti.

Kuitana Mbusa (115-123)

Anthu atafuka kuitana mbusa patchalitchi, achite zinthu izi:

1. Akumane ndi DS. ndi kusankha dzina la mbusa yemwe akumufuna ndipo kenako anthu akavote kutchalitchiko pa dzina limenelo. Aitane mbusa oti ali ndi chiphatso cha distilikiti kuti akhale mbusa. Komiti ya mpingo ikambilane ndi mtsogoleri wa chigawo za mbusa amene akumufuna pa tchalitchipo. Akatero amavota ndipo munthu amene akuitanidwayo amafunika kuti apeze mavoti ambiri kuti aitanidwe. DS. amayenera kuti avomereze munthuyo. (115)
2. Kenako dzinalo limaperekedwa ku tchalitchi kumene anthu amakavota mawu akuti ‘inde’ kapena ‘ayi’. Kuti munthuyo asankhidwe amayenera kupeza mavoti oposa theka a anthu omwe anavota.
3. A komiti ya pa tchalitchipo amamudziwitsa mbusayo kuti akumufuna pa tchalitchipo. Amayeneranso kuti amuwuze ndalama zoti azidzamupatsa ndi zinthu zimene iwowo akuyembekeza kwa iyeyo. (115.4)
4. Mbusayo amafunika kuti ayankhe pasanathe masiku khumi ndi asanu. (115.1)
5. Nthawi zina DS ndi a Adivaizale Komiti akhonza kusankha mbusa woti apite pa tchalitchi ngati chimodzi mwa izi chitachitika:
    a. Ngati mpingowo usanathe zaka ziwiri.
    b. Ngati mpingowo uli ndi anthu osakwana 35
    c. Ngati distilikiti ikuthandiza kulipira mbusa wa patchalitchipo.

Kusiya Ntchito Kwa Mbusa (120)

Mbusa akhonza kusiya ntchito pa kulemba kalata yosiyira ntchito ndi kuipereka ku komiti ya tchalitchi ndi kwa a DS. A komiti ya pa tchalitchi atavomereza ndi a DS akavomera kudzera mu kulemba kalata, ndiye kuti basi mbusayo atha kusiya ntchito. Komabe mbusayo amafunika kuti apitirize kugwira ncthito ya pa tchalitchipo kwa masiku makumi atatu (30) atamuvomera a komiti ndi DS kuti asiye ntchito.

Mbusayo adzagwira ntchito limodzi ndi mlembi wa pa tchalitchipo kukonza ndondomeko ya kaundula wa maina a amamembala a pa tchalitchipo pamodzi ndi ma keyala a anthuwo. Nambala ya anthu ya mkaundulayi iyenera ikhale yofanana ndi nambala imene yaperekedwa ku distilikiti.

Mgwirizano wa Pakati pa Mbusa ndi Mpingo (122)

Pa zaka ziwiri zili zonse mbusa ndi a komiti azikumana kuti awone pangano limene adapangana pa zomwe iwo amayembekezera kwa mbusayo, zolinga zawo, ndi mmene tchalitchi ndi mbusa uja achitila.

A DS ndi wofunika kudziwitsidwa za kukumana kumeneku kuti adzapezekepo. Cholinga cha kukumana uku ndi kuwona mavuto ndi kusiyana maganizo komwe kungapezeke, ndi ntchito ndi kuthetsa mavutowo mwa mtendere, mwa kulolerana ndi kukhululukirana. (121)

Kuwonjezera Nthawi ya Mbusa (123)

Mbusa akatha zaka ziwiri ali patchalitchi, padzakhala kukumana kwa a komiti kuti awone mmene mbusayo wagwilira ntchito. Kukumana kumeneku wotsogolera ndi a DS, kapena mbusa wodzozedwa kapena Leyimani amene a DS angamusankhe pa nthawiyo. Cholinga chake ndi kuti anthu agwirizane chimodzi popanda kuchita voti. Ngati a komitiwo akhutitsidwa ndi momwe mbusayo wachitira, amuonjezele zaka zina zinayi (4) kuti akhale patchalitchipo.

Akomiti akhonza kuchita voti kuti akanene nkhaniyo ku mpingo kwa anthu. Nthawi zina mpingo utha kuitanitsa msonkhano wapadera wampingo wonse kuti awafunse anthu. Ndiye ngati

mbusayo sanapeze mavoti oposa theka la anthu omwe avotawo, ndiye kuti basi mbusayo achoke pa nthawi yomwe wapatsidwa ndi a DS koma ngati wapeza mavoti oposa theka ndiye kuti basi apitilize ntchito yake ya pa tchalitchipo.

Gulu La Otsogolera Tchalitchi (127)

Mpingo uli wonse umakhala ndi komiti. Mamembala a komiti ndi awa:

1. Mbusa
2. Sande Sukulu Superintendent
3. Mtsogoleri wa NYI
4. Mtsogoleri wa NMI
5. Adindo ndi asungi (stewards and trustees)

Nthawi Yokambirana a Komiti (128)

A komiti ayenera kukumana pasanafike pa 15 pa mwezi uli wonse.

Ntchito ya a Komiti (129- 134)

1. Kuthandizana ndi mbusa kuyang'anira ntchito ya patchalitchi.
2. Kuitana mbusa ngati palibe patchalitchipo:
    - Asankhe munthu, ndipo atatenga chilolezo kwa DS apereke dzina la munthuyo ku mpingo kuti achite voti.
    - Kuwonjezera malipiro a mbusa chaka chili chonse.
3. Kusankha:
    - Msungichuma wa tchalitchi
    - Mlembi wa tchalitchi
    - Mamembala a bungwe la kufalitsa uthenga ndi komiti yowona za umembala

4. Kuwonetsetsa kuti ndondomeko ya chuma ya ku distilikiti, maphunziro ndi bungwe la kufalitsa uthenga la dziko lonse ikuperekedwa.
5. Kuwonetsetsa kuti ndalama zonse za pa tchalitchi zikugwira ntchito yake moyenera ndi kupereka malipoti mwezi uli wonse azokambirana za komiti, ndi kukapereka lipoti ku msonkhano wa pachaka wa chigawo (distilikiti).
6. Kusankha anthu awiri oti aziwerenga ndalama za chopereka sabata iliyonse.
7. Kukonza ndondomeko ya ndalama za ntchito ya pa tchalitchi chaka chili chonse.
8. A komiti a pa tchalitchi akhonza kuyenereza munthu kuti alandire chiphatso cha mlaliki ngati mbusa wa patchalitchipo ali wodzozedwa.
9. Kuyenereza munthu amene ali ndi chiphatso cha mlaliki kuti chiphatso cha distilikiti.

Mlembi wa Mpingo (135)

Ntchito ya mlembi wa tchalitchi ndi:

1. Kulemba zokambirana za tchalitchi ndi za a komiti.
2. Kupereka lipoti pa zokambirana za tchalitchi la za ntchito za patchalitchi kuphatikizapo chiwerengero cha mamembala a patchalitchi.
3. Kuyang'anira/kusunga malisiti ndi mapepala onse okhudzana ndi tchalitchiyo.
4. Pa nthawi yovotela mbusa, mlembi ndiye amakadziwitsa a DS momwe zayendela.

Msungi Chuma wa Tchalitchi (136)

1. Kulandila ndalama za tchalitchi ndi kulipila ndalama kumene tchalitchi iku yenera kulipila, molamudiwa ndi akomiti.
2. Kulembela ndalama zonse zolowa ndi zotuluka mu buku la zachuma.

3. Kupereka lipoti la zachuma pa kukumana kwa komiti mwezi uli wonse ndi pa kukumana kwa tchalitchi yonse chaka chili chonse.

Adindo (Stewards) (137-140)

Komiti iyi imakhala ndi anthu osachepela atatu koma osapitilila khumi ndi atatu. Ntchito yawo ndi:

1. Kukhala komiti ya tchalitchi yowona za kukula kwa tchalitchi ndi maudindo a kufalitsa uthenga, kutchitila umboni ndi kubzala mipingo yatsopano.
2. Kupereka chithandizo kwa anthu osowa ndi ovutika. Amafunika kuti azipereka chilimbikitso, kuyendela anthu, kusamalira odwala ndi osowa ndi kuphunzitsa akhristu za utumiki wothandiza osowa.
3. Akhonza kukhalanso komiti yowona za umembala wampingo.
4. Kuthandiza kukonza pulogalamu ya mgonelo.
5. Kukhala komiti yowona za kukhulupilika kwa akhristu ndi kulimbikitsa anthu kuti azipereka mowolowa manja, nthawi yawo, maluso awo ndi ndalama zawo ku ntchito ya Ambuye.

Asungi (Trustees) (141 — 144)

Pakhale asungi osachepela atatu ndipo asapitilile 9. Ntchito yawo ndi kuyang'anira malo ndi nyumba za tchalitchi. Ntchito yawo ina ndi kuti aziwona njira zimene tchalitchi ingapezele ndalama ndiponso chakuti mbusa akhale omasuka kupereka nthawi yake yonse ku zosowa za uzimu za pa tchalitchi.

Komiti Yowona za Sande Sukulu Ndi Kuchitira Umboni (145)

Mu mipingo momwe muli anthu osakwana 75, a komiti ya tchalitchi akhonza kuimira komiti yowona za Sande Sukulu. Komiti imeneyi ili ndi udindo woyangánira ntchito ya Sande Sukulu, kalabu

yowona mautumiki onse a maphunziro a Buku Lopatulika ndi kuphunzitsa mu mpingo.

Ntchito yawo ndi yoti afikire anthu ambiri omwe asanamve uthenga, kuwabweretsa mu chiyanjano cha mpingo, kuphunzitsa Mawu a Mulungu mwa khama, kuphunzitsa ziphunzitso za mpingo wa chikhristu ndi kupanga anthu ofanana ndi Yesu mu chikhalidwe, malingaliro, kukonzekeletsa okhulupilira kukhala mamembala mu mpingo ndi kuwasula kuti akachite ntchito ya utumiki mu mpingo wa Khristu.

Nazarene Youth International (NYI) (150 — 151.5)

Bungwe la NYI limagwira ntchito pa tchalitchi kuti lithandize ndi kulimbikitsa achinyamata. Cholinga cha NYI, ndi:

- Kuthandiza achichepele kuti alandire Yesu ngati mpulumutsi wawo.
- Kulangiza achinyamatawo mu Mawu a Mulungu ndi ziphunzitso za mpingo.
- Kuwathandiza kuti akule mu moyo wawo wauzimu ndi moyo wachiyero.
- Kuwathandiza kuti akhale mamembala ndi kukhala ochitachita mu mpingo.
- Kusula achinyamata kuti akhale otenga nawo mbali mu utumiki.

Achinyamata pa tchalitchi akhonza kusankha komiti ya NYI, imene ili ndi mtsogoleri wachiwiri wake, mlembi ndi msungichuma. Anthu osankhidwa mu ma udindo onsewa akhale mamembala a mpingo.

Zambiri zokhudza bungwe la NYI zili mu buku la malamulo la NYI (NYI Constitution)

Nazarene Mission Internatinal (NMI) (153 — 155.3)

Bungwe la NMI limagwira ntchito pa tchalitchi kuti libale chilakolako chaku pempherera ndi kuthandiza a Mishoni a Mpingo omwe ali m'maiko ena. Cholinga cha NMI ndi:

1. Kulimbikitsa anthu kuti azipempherera anthu omwe asadapulumutsidwe.
2. Kudziwitsa mpingo za momwe ikuyendela ntchito ya Mulungu m'maiko ena.
3. Kuthandiza achinyamata kuti amve maitanidwe ndi kudzipereka ku ntchito ya Mulungu.
4. Kulimbikitsa anthu kuti azipereka mowolowa manja kuntchito ya kufalitsa uthenga ku dziko lapansi.

NMI izisankha komiti yomwe izikhala ndi anthu awo, mtsogoleri, wachiwiri kwa mtsogoleri, mlembi, msungichuma ndi maudindo ena omwe angafunike. Zina zokhudza bungwe la NMI zili mu buku la malamu a NMI (NMI Constitution).

Bungwe la Chigwirizano cha Amayi ndi Bungwe la Chiyanjano cha Abambo

Chigwilizano cha amayi ndi chiyanjano cha abambo mulibe mu Manyo. Komabe mabungwe awiliwa akhonza kuikidwa pa tchalitchi monga momwe alili mabungwe a NMI ndi NYI. Zikhonza kukhala bwino kuti atsogoleri a mabungwe awiliwa akhale ochokela mu komiti ya tchalitchi monga momwe ilili NYI ndi NMI, kuti atsogoleri ake ndi a mu komiti ya tchalitchi.

Mpingo wa Nazarene pa Chigawo (Distilikiti) (200 — 205)

Msonkhano wa Chigawo

Matchalitchi angapo a mu dera amaphatikizidwa ndi kupanga chigawo (Disilikiti). Pali magulu atatu a ma distilikiti mu mpingo wa Nazarene. Magulu ake ali motere:

Gulu 1:

Mpingo wa Nazarene ukakhala kuti ukuyamba kumene mu dziko lina lake kapena mu dera lina latsopano, chigawo (distilikiti)

chimakhala mu Gulu 1. Mkulu woyang'anira chigawo chachikulu (Rijoni) adzapereka dzina la munthu kwa GS (General Superintendent) woti akhale woyang'anira distilikiti (District Superintendent). Kenako GS (General Superintendent) adzatenga dzinalo ndi kulivomereza kuti munthuyo akhale DS wa chigawocho.

Gulu 2:

Distilikiti yomwe ili mu Gulu 2 ndi imene ili ndi mipingo yosachepera khumi yokhazikika, mamembala okwana 500 ndi abusa odzozedwa okwana 5. Theka la ndalama zoyendetsera distilikiti (chigawo) zimachokera mu distilikiti momwemo. Munthu akhonza kuvoteledwa kapena kungolozedwa kuti akhale DS.

A Disilikiti Adivazale Komiti akhonza kupempha kuti distilikiti yawo ilowe mu Gulu 2. Mkulu woyang'anira ma distilikiti ndi ma DS. (Field Director), mkulu wa chigawo chachikulu ndi GS (General Superintendent) akapereka pempholi kwa komiti yayikulu ya dziko lonse. DS akhonza kuvoteredwa kapena kungolozedwa ndi chala.

Gulu 2 la Chigawo	**D.S.** akhonza kutchulidwa kapena kusankhidwa	
Zofunikira	Matchalichi khumi Okhazikika	Abusa Asanu Odzodzedwa
	Mamembala 500	50% modzithandiza okha zinthu za Chuma

Gulu 3:

Distilikiti ya mu Gulu 3 ndi yomwe yawonetsa kuti ili ndi atsogoleri okhwima, yokhazikika pa chuma, yotsatira bwino ziphunzitso za mpingo ndipo ili ndi masomphenya a kukula kwa mpingo dziko lonse lapansi.

Distilikiti ya mu Gulu 3 imayenera kukhala ndi mipingo yokwana 20 yokhazikika bwino, mamembala 1,000, abusa odzozedwa okwana 10 ndi kudzipezera ndalama zoyendetsera distilikitiyo payokha.

DS wa distilikiti ya mu Gulu 3 amachita kuvoteredwa pa msokhano wa pa chaka.

Msonkhano wa pa Chaka wa Chigawo

Anthu ofunika ku msokhano wa pa chaka ndi awa:

- Abusa onse odzozedwa.
- Abusa omwe ali ndi ziphatso
- Mlembi wa chigawo
- Msungichuma wa chigawo
- Mkulu wa Sande Sukulu
- Mtsogoleri wa NYI wa chigawo
- Mtsogoleri wa NMI wa chigawo
- Atsogoleri a Sande Sukulu ama tchalitchi
- Atsogoleri a NYI a m'matchalitchi
- Atsogoleri a NMI a m'matchalitchi
- Ma leyimani omwe ali mu Adivazale Komiti
- Nthumwi zochokela ku mipingo yonse

Nambala ya Anthu Opita ku Msonkhano wa pa Chaka

Mpingo Umene uli ndi Anthu Oyambila:

1- 50 - Nthumwi ziwiri
51 - 100 - Nthumwi zitatu
101 - 150 - Nthumwi zinayi
151 - 200 - Nthumwi zisanu

Izi zikutanthauza kuti pa mpingo pakhonza kuchoka anthu awa kupita ka nsokhano wa pa chaka:

1. Mbusa ngati ndi odzozedwa kapena ali ndi chiphatso.
2. Sande Sukuku Superintendent
3. Mtsogoleri wa NYI

4. Mtsogoleri wa NMI
5. Nthumwi zosankhidwa ndi mpingo kutengerana ndi kukula kwake kwa mpingowo.

Nthawi ya Msonkhano wa pa Chaka
Nthawi ya msonkhano wa pa chaka amaika ndi GS (General Superintendent).

Ntchito Ya Msonkhano wa pa Chaka
Kumva malipoti kuchokera kwa:

1. Abusa onse odzozedwa ndi aziphatso
2. DS
3. Msungichuma wa chigawo
4. Komiti ya distilikiti (chigawo)
5. Mkuku wowona za maphunziro a ubusa
6. Bungwe la za maphunziro
7. Bungwe lowona za kudzoza abusa

Msonkhano wa pa chaka umasankha atsogoleri awa ndi ma komiti awa:

- Mtsogoleri wa Chigawo (203.11)
- Bungwe La Alangizi A Chigawo DAB (203.14)
- Bungwe lowona za kudzodza (203.15)
- Komiti yowona za maphunziro (203.16, 203.17)
- Bungwe Lowona za maphunziro a Sande Sukulu (203.20, 237)
- Bungwe Lowona za Katundu (203.18)

Ntchito inanso yochitika pa msonkhano wa pa chakawu ndi:

- Kupereka ziphatso kwa abusa (203.4)
- Kupereka maina a abusa oti adzozedwa (203.6 203.7)
- Kulandira abusa ochoka ku mipingo ina kuti akhale abusa mu mpingo wa Nazarene.

- Kuwunika lipoti la ndalama la momwe distilikiti yagwiritsira ntchito, ndi kulivomera lipoti

Mtsogoleri wa Chigawo - DS (206-214.1)

Mtsogoleri wa Chigawo akhale mbusa woti adadzozedwa. Itakhala disilikiti ya mu Gulu 1, Mtsogoleri wa Chigawo amachita chosankhidwa ndi Jenolo Superintendenti. Itakhala disilikiti ya mu Gulu 2, Mtsogoleri wa Chigawo akhonza kusankhidwa ndi Jenolo Superintendenti kapena anthu akhoza kuvotera munthu yomwe akumufuna.

Mu distilikiti ya mu Gulu 3, Mtsogoleri wa Chigawo amachita kuvoteredwa. Patatha zaka ziwiri, Mtsogoleri wa Chigawo akhonza kuvoteledwanso. Izi zikhonza kuchitika ndi mavoti a "inde kapena ayi". Kuti Mtsogoleri wa Chigawo aimenso pa mpando wayanera kupeza mavoti oposela theka la mavoti onse. Ngati wasankhidwanso ndiye kuti akhala pa mpando kwa zaka zina zinayi. Ngati Mtsogoleri wa Chigawo wasiya ntchito kapena wachotsedwa pa mpando ndi mavoti, ndiye kuti Mtsogoleri wa Chigawo wina watsopano asankhidwenso kuti alowe m'malo mwa winayo. Mu distilikiti imene ili mu Gulu 3, nthumwi zikhonza kuvotera mbusa wina aliyense wodzozedwa wa mpingo wa Nazarene. Kuvota kuzipitilira ngati asanapezeke amene wapeza mavoti oposa theka mpaka wina apezeke ndi mavoti ochuluka oyenera ndi mlingo wake.

Ntchito ya Mtsogoleri wa Chigawo (DS)

Ntchito ya Mtsogoleri wa Chigawo ikhonza kugawidwa mu magawo awiri akuluakulu:

1. Kugwira Ntchito ndi Matchalitchi onse Amene ali mu Chigawo Chake

- Kukonza ntchito ya matchalitchi, kuthandiza ndi kulimbikitsa, matchalitchiwo. (208.1)
- Kukumana ndi ma komiti am'matchalitchi kuti awunike momwe abusa agwiira ntchito. (121, 208.2)

- Kukumana ndi makomiti a m'matchalitchi ndi abusa kuti apereke uphungu wa chitsogozo pa moyo wauzimu, nkhani za ndalama ndi zina zokhudza abusa. (208.3)
- Kupereka uphungu ndi chitsogozo ku mipingo yongoyamba kumene. (208.6)
- Ngati mbusa wa patchalitchi ndi osadzozedwa, ndiye kuti Mtsogoleri wa Chigawo ndi amene angayeneleze munthu amene akufunika kulandila chiphatso cha mlaliki. (208.12)
- Mtsogoleri wa Chigawo akhonza kukhala pa tchalitchi ngati mbusa wa patchalitchiyo
- Mtsogoleri wa Chigawo akhonza kuchititsa msonkhanoso wa pa chaka wa zokambilana pa tchalitchi
- Akhonza kuvomereza zopempha zochita kulemba mu kalata kuchoka kwa abusa ndi matchalitchi zoti alembe ntchito anthu ena othandiza pa tchalitchi monga a utumiki wa a chinyamata, wachiwiri kwa abusa ndi ena.

2. Mtsogoleri wa Chigawo (DS) ali ndi Udindo Wogwira Ntchito izi mu Distilikiti:

- Kukhala wapa mpando wa Adivaizale Komiti.
- Kuchititsa msonkhano wa pachaka ngati palibe Jenolo Superintendenti.
- Kukhala membala wa mabungwe ndi makomiti onse apa disilikiti.
- Ngati mtsogoleri wa distilikiti wasiya udindo wake, DS akhonza kusankha munthu wina woti alowe m'malo mwa munthuyo, mwachitsanzo, mlembi wa distilikiti (208.7),, msungichuma wa disilikiti (208.8).

Mlembi wa Chigawo (216 — 218)

Mlembi wa distilikiti amasankhidwa ndi Adivaizale Komiti kuti agwire ntchitoyo kwa zaka zitatu ndipo akhonza kusankhidwanso pakutha kwa zaka zitatuzo. Mlembi akuyembekezedwa kugwira ntchito izi:

1. Kulembela ndi kusunga zokambilana za distilikiti ndi zina za msonkhano wa pachaka.
2. Kusunga mbiri ya zochitika za pa distilikiti.
3. Kutumiza malipoti ku likulu la ma distilikiti (field office).
4. Kuyang'anira mapepala ndi ma lisiti onse a distilikiti.

Msungi chuma wa Distilikiti (219 — 220.2)

Msungichuma wa distilikiti amasankhidwa ndi Adivaizale Komiti. Ntchito za msungichuma ndi izi:

1. Kulandira ndalama zonse zobwera ku distilikiti ndi kuzigawa ndalamazo ku ntchito zosiyanasiyana malinga ndi momwe akonzera a Adivaizale Komiti ndi msonkhano wa pa chaka.
2. Kulembera ndalama zolowa ndi zotuluka ndi kupereka lipoti la ndalamazo kwa a DS mwezi ndi mwezi, ndi ku msonkhano wa pachaka wa chigawo.

Gulu la Alangizi a Chigawo (Disilikiti adivaizale) (221-225)

Mamembala a komiti iyi amasankhidwa chaka chilichonse pa msokhano wa pa chaka. Mamembala ake ndi awa:

- DS
- Abusa odzozedwa atatu
- Ma leyimani atatu

Ma distiliki omwe ali mu Gulu 1 ndi 2, Filudi dailekita (Field Director) akhonza kusankha nthumwi yoyimila Mishonale mu Adivaizale Komiti. DS ndiye wapampando wa Adivaizale Komiti:

Ntchito ya Adivaizale ndi:

1. Kuika nthawi yoyambira ndi kumaliza kugwiritsa ntchito ndalama za mu distilikiti.
2. Mamembala amu adivaizale Komiti amakambirana ndi a DS zokhudza abusa ndi matchalitchi. Amaperekanso uphungu kwa komiti iliyonse ya mu distilikiti.
3. Kusankha mlembi ndi msungichuma wa distilikiti (chigawo).
4. Ngati mbusa amene ali ndi chiphatso ali pa tchalitchi, a Adivaizale Komiti avomereze chiphatsocho kuti achiwonjezere nthawi.
5. Ngati munthu wina atabweretsa nkhani yonena mbusa kuti sakuyenda bwino, Adivaizale Komiti isankhe komiti yoti ifufuze nkhaniyo; ngati ndi yowona komitiyo ikhale ya abusa atatu adzozedwa, kapena akhonza kuposela apo.
6. Adivaizale ili ndi udindo woyang'anira katundu ndi nyumba za distilikiti.
7. Mbusa wochoka ku mpingo wina atafuna kulowa mpingo wa Nazarene, a Adivaizale aone masatifiketi omwe ali nawo ndipo ngati wavomerezedwa, akhonza kulandilidwa kukhala chida cha mpingo.

Mu ma distilikiti omwe ali mu Gulu 3, pamakhala ma komiti osiyanasiyana ambiri. Ndime zotsalilazi zikufotokoza za ma komitiwa:

1. Komiti Yoyenereza Kulandira Ziphatso Kapena Kudzozedwa (226-228.10)

Komiti iyi imakhala ndi abusa odzozedwa osachepela asanu (5) ndipo osapitilira khumi ndi zisanu (15). DS amakhala m'modzi mwa mamembala a komiti, ndipo mamembala amasankhidwa kwa nthawi ya zaka zinayi. DS amakhala wa mpando wa komiti koma amatha kuwuza a komitiyo kuti asankhe munthu wina kuti akhale wapampando wa komitiyo. Komitiyo imasankha mlembi woti azilemba zomwe akambirana.

Ntchito ya komiti imeneyi ndi:

1. Kuwunika zomuyenereza munthu amene akufuna kulandira chiphatso kapena kudzozedwa.
2. Kufufuza ngati munthuyo adapulumutsidwa, amayenda moyo wa chiyero, ndi wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, Buku Lopatulika amalidziwa mokwanira, ziphunzitso za mpingo, kusunga malamulo odziwika ndi malamulo apader+a a mpingo, umboni wa mphatso za Mzimu Woyera, khalidwe la umunthu ndi kuwona ngatidi utumiki angauthe.
3. Ngati munthu ali ndi chiphatso cha mlaliki ndipo adakhalako pa tchalitchi ngati mbusa, ndiye kuti a komitiyo amuvomereze msangamsanga kupitiliza kutumikira ngati mbusa.

2. Komiti Yowona za Maphunziro (229-231.4)

Komitiyi imakhala ndi abusa odzozedwa asanu (5) kapena kuposera pamenepo. Amasankhidwa ndi msokhano wa pa chaka wa chigawo (distilikiti); kuti atumikire kwa zaka zinayi (4).

Komitiyi idzasankha wa pa mpando ndi mlembi wake. Ntchito ya komiti imeneyi ndi kuyang'anira maphunziro a anthu akufuna kuti adzozedwe. Alinso ndi udindo wolimbikitsa, kuthandiza ndi kutsogolera amene akuchita maphunziro.

3. Komiti Yowona za Katundu wa Mpingo pa Distilikiti (233-234.5)

Komiti imeneyi ndi yokhala ndi DS, abusa awiri odzozedwa ndi ma Leyimani awiri. Mamembala a komitiyi akhonza kusankhidwa kutumikira kwa zaka zinayi (4). Adivaizale Komiti ikhonza kutenga udindo wa komiti imeneyi.

Ntchito ya komiti yowona za katundu wa mpingo ndi kulangiza DS ndi matchalitchi nkhani zokhudza malo, mapulani a mamangidwe anyumba za mpingo ndi mapulani omanga matchalitchi. Ndondomeko ili yonse yomanga tchalitchi yayenera kudzera kwa owona za katundu wa Mpingo kuti avomereze kumanga kusanayambike.

4. Komiti Yowona za Sande Sukulu pa Distilikiti (237-238.3)

Komiti iyi imakhala ndi mamembala awa:

- DS
- Mtsogoleri wa NMI
- Mtsogoleri wa NYI
- Wa pa mpando wa komiti ya Sande Sukulu ndi mamembala ena atatu ochita kusankhidwa.

Ukangotha msonkhano wa pa chaka komiti idzakumana ndi kusankha anthu awa:

- Mlembi
- Msungichuma
- Mkulu wowona za utumiki wa akuluakulu mu chigawo
- Mkulu wowona za utumiki wa ana mu chigawo

Anthu amenewo adzakhala mamembala a komiti yowona za Sande Sukulu mu chigawo. Komitiyi ili ndi ntchito yoyang'anira maphunziro a Sande Sukulu mu chigawo.

5. Bungwe la Ulangizi pa Distilikiti (District Adivisory Council)

Makomiti onse atakumana, amapanga bungwe la ulangizi la mu disilikiti. Amayenela kukumana miyezi isanu ndi chimozi (6) ili yonse kuti akambirane za njira zimene zingathandize kuti ntchito ya mpingo ipite patsogolo.

Mpingo wa Nazarene ku Lukulu

Msonkhano Waukulu Wa Mpingo Wonse

Msonkhano waukulu Wa Mpingo Wonse ndi Msonkhano wofunika kwambiri mu Mpingo wa Nazarene. Uli ndi mphamvu zopanga chiphunzitso ndi zikhulupiriro za mpingo ndi malamulo oyendetsera mpingo pa dziko lonse lapansi. Atsogoleri A Mpingo Wonse (General Superintendents) ndi amene amakhala apa mpando a msonkhanowo.

Nthumwi zopita ku Msonkhano Wa Ukulu Wa Mpingo Wonse ndi izi:

1. Nthumwi zosankhidwa kukaimira distilikiti ya fezi 3, zidzakhala theka limodzi la abusa adzozedwa ndi theka lina ma akhristu osakhala abusa.

Disilikiti yomwe ili ndi anthu oyambila:

Mamembala	**Abusa Odzozedwa**	**Maleyimani**
1 - 2000	1 (DS)	1
2001 - 5500	DS ndi mbusa m'modzi	2
5501 - 9000	DS ndi abusa awiri	3

2. Chigawo chimene chili mu fezi 2 chikhonza kutumiza DS ndi mkhristu m'modzi amene asali m'busa.
3. Chigawo chomwe chili mu fezi 1 chikhonza kutumiza DS koma DS alibe mwayi wokavota nthawi ya masankho.
4. Atsogoleri A Ukulu A Mpingo Wonse
5. Mlembi Wankulu Wa Mpingo Wonse
6. Msungichuma Wamkulu Wa Mpingo Wonse
7. Mkozi wa "Holiness Today"
8. Mtsogoleri wa NYI, wa Dziko Lonse.
9. Mtsogoleri wa NMI wa Dziko Lonse.
10. Atsogoleri a Zigawo Zazikulu (Ma Rejoni)

Nthawi ya Kukumana (302)

Msonkhano Wa Ukuluwu umachitika mu mwezi wa Juni pa zaka zinayi (4) zili zonse, mwachitsanzo, 2009, 2013, 2017 motere.

Ntchito ya Msonkhano Wa Ukulu Wa Mpingo Wonse (305)

1. Kusankha Atsogoleri A Akulu A Mpingo Wonse okwana asanu ndi mmodzi (6) ndi mavoti 2/3 amavotiwo.
2. Kusankha mamembala a komiti ya Yikulu Ya Mpingo Wonse.

Ma distilikiti akhonza kutumiza maganizo awo pa zinthu zomwe akufuna kuti zisinthe mu Buku La Malamulo Ndi Mayendetsedwe A Mpingo Wa Nazarene kapena malamulo. Maganizowa adzatumizidwa ku ma komiti a Msonkhano Wa Ukulu

Wa Mpingo Wonse kuti akambirane. Ma komitiwa adzavomereza zinthu zoti zisinthe ndi zoti zisasinthe, ndipo iwo adzatumiza zinthuzo ku Msonkhano Wa Ukulu Wa Mpingo Wonse kuti Msonkhawo ukambiranenso nkhaniyo. Msonkhanowo utatha kukambilana udzachita voti. Umu ndi m'mene Buku La Malamulo Ndi Mayendetsedwe A Mpingo Wa Nazarene limasinthidwira kapena kukonzedwanso.

11. Atsogoleri A Ukulu A Mpingo Wonse (306-307.14)

Atsogoleri A Akulu A Mpingo Wonse okwana asanu ndi m'modzi (6) amayenela kukhala abusa odzozedwa. Amayenera kukhala munthu wa zaka zosachepela 35 zakubadwa koma zosapitira 68. Amasankhidwa ku Msonkhano Wa Ukulu Wa Mpingo Wonse. Ntchito yawo ndi iyi:

1. Kuyang'anira ntchito ya Mpingo Wa Nazarene padziko lonse lapansi.
2. Kukhala a pa mpando a zokambirana za pa Msonkhano Wa Ukulu Wa Mpingo Wonse.
3. Amagwira ntchito kuthandiza ma distilikiti:

- Kukhala wa pa mpando wa Msonkhano W Chigawo wa pachaka wa distilikiti kapena kusankha munthu kuti akhale wa pa mpando.
- Kudzoza abusa omwe distilikiti yawavomereza kuti adzozedwe kapena kuwuza munthu wina kuti achite ntchitoyo.
- Akhonza kusankha munthu kuti akhale DS ngati papezeka kuti DS wachoka nthawi ya msonkhano wa pa chaka isanafike. Izi amachita atakambirana ndi Alangizi A Chigawo ndi atsogoleri a NMI ndi NYI ndi wa pa mpando wa komiti ya za Sande Sukulu, komanso ndi Mlembi ndi Msungichuma Wa Chigawo. (onani 207)

Bungwe La Atsogoleri A Akulu A Mpingo Wonse (315 — 324)

Bungwe La Atsogoleri a Akulu A Mpingo Wonse (GS) limakumana kamodzi pa miyezi itatu iliyonse.

1. Limayang'anira ntchito ya Mpingo wa Nazarene pa dziko lonse lapansi. Mpingo wa Nazarene udagawidwa mu

zigawo zisanu ndi chimodzi (6) ma Rejoni ndipo Mtsogoleri Wa Mkulu Wa Mpingo Wonse aliyense ali ndi chigawo chake chimene amayang'anira.

2. Kuyang'anira makomiti onse oyendetsa mpingo ku dziko lapansi, pamodzi ndi mabungwe ena onse amu mpingo ku dziko lonse.
3. Atsogoleri A Akulu A Mpingo Wonse ndi Komiti Yaikulu Ya Mpingo Wonse adzapanga ndondomeko ya momwe ndalama za ku bungwe la Kufalitsa Uthenga Ku Dziko Lonse Lapnsi (World Evangelism) zigwilire ntchito yake.
4. Komiti Yaikulu Ya Atsogoleri A Akulu A Mpingo Wonse idzakhala ndi mphamvu zotanthauzira malamulo ndi ziphunzitso za mpingo wa Nazarene.
5. Munthu amene banja lake latha ndiye akufuna kuti adzozedwe ndipofunika kuti Atsogoleri A Akulu A Mpingo Wonse awunike nkhani yake kuti awone ngati ndi koyenera kutero.
6. Ali ndi mphamvu kuchita china chili chonse chomwe akuwona kuti ndi chothandiza pa ntchito ya Mulungu ngati sichikutsutsana ndi malamulo a Mpingo wa Nazarene.

Mlembi Wamkulu Wa Mpingo Wonse (General Secretary) (325-328.1)

Mlembi wamkulu amasankhidwa ndi Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse. Mlembi wamkuluyi amayang'anilidwa ndi Atsogoleri A Akulu A Mpingo Wonse ndi Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse. Ntchito ya mlembi wamkulu ndi:

1. Kulemba zokambirana za pa msonkhano waukulu.
2. Kusunga nambala ya memembala onse a Nazarene dziko lonse mu kaundula.
3. Kusunga mosamala makalata amalamulo ndi makalata onse ofunikira a mpingo.

Msungichuma Wamkulu Wa Mpingo Wonse (329-330.7)

Msungichuma Wamkulu amasankhidwa ndi Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse. Msungichuma Wamkuluyi amayang'aniridwa ndi Atsogoleri A Akulu A Mpingo Wonse ndi Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse.

Ntchito ya Msungichuma Wamkulu ndi:

1. Kuyang'anira ndalama zonse zobwera ku likulu.
2. Kugawa ndalamazo ku ntchito zosiyanasiyana malinga ndi momwe yakonzela Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse.
3. Kupereka lipoti la ndalama zomwe zilipo ku komiti yayikulu pakutha kwa chaka.

Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse (331-336)

Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse imasankhidwa ku msonkhano waukulu. Msungichuma Wamkulu Wa Mpingo Wonse ndi Mlembi Wamkulu Wa Mpingo Wonse ndi ena mwa mamembala a Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse. Pali anthu okwana makumi a nayi (40) mu Komitiyi ndipo amakumana kamodzi pa chaka. Ma distilikiti osiyanasiyana a matchalitchi amagawidwa malinga ndi dera lomwe alili la dziko lapansi. Dera lili lonse likhonza kusankha mamembala a Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse. Awa amaka voteredwa ndi nthumwi za ku Msonkhano Waukulu Wa Mpingo Wonse za kudela lawolo.

Mamembala a Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse:

Kukula kwa Dela	**Maleyimani**	**Abusa**
Anthu okwana 100,000	1	1
Anthu okwana 100,001 - 200,000	2	2
Anthu oposa 200,000	3	3
Oyimira dziko lonse		
Wa NYI	1(m'modzi)	
Wa NMI	1(m'modzi)	
Woyimira ma koleji a Nazarene	1	1

Nchito ya Komiti Yayikulu Ya Mpingo Wonse

Komiti yayikulu imasamalira ntchito yonse ya mpingo ku dziko lonse. Imathandiza bungwe lili lonse kuti lizigwira bwino ntchito zake mogwirizana ndi ma bungwe ena.

Komiti yayikulu imapanga ndondomeko ya mmene ndalama za bungwe lofalitsa uthenga ku dziko lonse (World Evangelism) zingagwilire ntchito. Imagawa ndi kutumiza ndalama ku mabungwe osiyanasiyana a mpingo. Komiti yayikulu imamva ma lipoti kuchokera ku mabungwe onse a mpingo.

Mtumiki mu Mpingo wa Nazarene

Pali magulu atatu a atumiki mu mpingo wa Nazarene. Maguluwa ndi awa:

1. Mtumiki (mlaliki) wa pa tchalitchi amene wavomerezedwa ndi komiti ya pa mpingo.
2. Mtumiki wa mu chigawo wa chiphatso amene wavomerezedwa ndi msonkhano wa chigaw wa pa chaka.
3. Mbusa wodzozedwa amene wavomerezedwa ndi msonkhano wa pa chaka ndipo amadzozedwa ndi Mtsogoleri Wamkulu Wa Mpingo Wonse ndi abusa ena odzozedwa.

Mlaliki wa pa Tchalitchi (428)

1. Mlaliki wa patchalitchi amafunika kuti akhale membala wa mpingo wa Nazarene. Mlaliki amapatsidwa chiphatso ndi apa tchalitchi imene iyeyo ali membala, ndipo amagwila ntchito limodzi ndi mbusa wa pa tchalitchipo. Izi zimamupatsa mwayi munthuyo kuti agwilitse ntchito mphatso zake ndi kuzitukula. Akatero mtumikiyu amakhala kuti wayamba kuphunzira mu moyo wake ngati mtumiki.
2. Ngati mbusa wa pa tchalitchi ndi odzozedwa ndiye kuti a komiti a pa tchalitchipo akhonza kumupatsa chiphatso mtumikiyo chomwe chingasainidwe ndi mlembi ndi mbusa.

3. Ngati mbusa wa patchalitchi ndi wosadzozedwa, ndiye kuti pempho lakuti munthuyo alandire chiphatso livomerezedwe ndi Bungwe La Alngizi a Chigowo ndi Mtsogoleri Wachigawo.
4. Munthuyo awunikidwe bwinobwino ngati alidi opulumutsidwa, ziphunzitso za Buku Lopatulika akuzidziwa ndi Buku La Malamulo ndi Mayendetsedwe A Mpingo Wa Nazarene ngati akulidziwa bwino. Anthu oti apatsidwe chiphatso aziwonetsa kuti ali ndi mphatso za uzimu ndi kuti akhale wokhwima mu uzimu.
5. Chiphatso chimagwira ntchito kwa chaka chimodzi.
6. Mlalikiyu akuyenera kuchitira maphunziro a utumiki. Pakatha zaka ziwiri asanatsilize maphunzirowo ndiye kuti chiphatso chake chatha ntchito.
7. Chiphatso chikhonza kuwonjezeredwa nthawi ndi a komiti a tchalitchi pa umboni wa abusa. Ngati mbusa wa pa tchalitchi ndi wosadzozedwa, ndiye kuti mbusayo ndi akomiti a pa tchalitchi achitire umboni za munthuyo ndipo a Mtsogoleri Wachigawo avomereze kuti chiphatsocho achiwonjezere nthawi.
8. Mlaliki wa pa tchalitchi si woyenera kuti achititse ma sakirament a kubatiza ndi kudyetsa mgonero ndiponso sayenera kumangitsa ukwati.

Mtumiki wa Chiphatso wa pa Distilikiti (429)

1. Anthu ofuna kukhala ndi chiphatso akhale kuti ndi mamembala a mpingo wa Nazarene ndipo akhale kuti adamvadi maitanidwe a kutumikira.
2. Akhale kuti adalandilapo chiphatso cha mlaliki wa pa tchalitchi kwa chaka chathunthu.
3. Akhale munthu woti a komiti a patchalitchi yake akuchitira umboni kuti iyeyo ndi membala. Ngati munthuyo akutsogolera mpingo, ndiye kuti a Adivaizale Komiti amuvomereze kuti alandile chiphatso.

4. Akhale munthu woti watha chaka ali ku sukulu ya ubusa kapena kuti wamaliza maphunziro okwana 8 a utumiki.
5. Alembe bwino fomu yolandirila chiphatso ndipo aipereke kwa Bungwe La Chigawo Losungitsa Mwambo mu Mpingo kuti alandile chiphatso kapena kudzozedwa.
6. Achite maphunziro a zautumiki operekedwa ndi Buku Lopatulika, koleji kapena a distilikiti.
7. Ngati akuyang'anira mpingo, azipereka malipoti mwezi ndi mwezi kwa DS.
8. Munthuyo adzafunsidwa mafunso ndi Bungwe La Chigawo Losungitsa Mwambo mu Mpingo alandile chiphatso kuti amuwone ngati ali woyenera kukhala mtumiki.
9. Munthuyo wayenera kupeza mavoti okwanira pa msonkhano wa pa chaka wa chigawo.
10. Chiphatso chimagwira ntchito chaka chimodzi.
11. Atumiki omwe ali ndi ziphatso amene akutumikira ngati abusa ndipo adachita maphunziro ofunikira, adzakhala ndi mphamvu za kulalikila, kudyetsa mgonelo, kubatiza ndi kumangitsa ukwati ku matchalitchi kwawo.
12. Atumiki amene ali ndi chiphatso ochokela ku mipingo ya chi Evanjeliko azipereka makalata awo, ndipo akhale kuti maphunziro omwe adachita ndi ofanana ndi omwe amaphunzitsa a Nazarene, ndipo akwaniritsa zonse zofunika zimene tanena kale, akhonza kupatsidwa chiphatso.

Munthu akalandira chiphatso, achite zinthu izi kuti chiphatso chikhalebe ndi mphamvu pakuchiwonjezera nthawi:

1. Azifila fomu chaka ndi chaka yoti awonjezera nthawi ya chiphatsocho.
2. Ayenerezedwe ndi a Adivaizale Komiti.
3. Awonjezere maphunziro ena awiri kapena kuposa a po mu maphunziro ake.
4. Ngati akuyang'anira mpingo, azipereka ma lipoti kwa a DS mwezi uliwonse.

5. Awonetse kuti ali ndi chisomo, mphatso ndi kuti ndi wothandiza pa ntchitoyo.
6. Ayenerezedwe ndi Bungwe La Chigawo Losungitsa Mwambo mu Mpingo pa msonkhanao wa pa chaka.
7. Akhale ndi cholinga chofuna kudzozedwa ngati mbusa kapena dikoni mu mpingo wa Nazarene. Munthu amene ali ndi chiphatso sangachiwonjezeretso nthawi patatha zaka 10 (khumi) pokhapokha ngati pali zifukwa zina.

Dikoni (430)

Dikoni ndi munthu amene amamva maitanidwe ku ntchito ya Mulugu, koma osati maitanidwe akulalikila. Ma dikoni ena amakatumikira ku zipatala monga wamkulu wa mapemphero (tchapuleni), ena amachita utumiki woyendera anthu mu matchalitchi omwe ndi akuluakulu kapena amaikidwa mu bungwe la zachifundo.

Dikoni amapatsidwa mphamvu kuti akhonza kuchititsa ma sakilamenti ndi kulalikira ndi kuchititsa mapemphero nthawi zina.

Njira zotsata kuti munthu adzozedwe ngati dikoni ndi chimodzimodzi ndi njira zakuti munthu akhale mbusa wodzozedwa.

M'busa Odzodzedwa (431)

Udindo wa kukhala mbusa wodzozedwa ndi wa anthu omwe adamva maitanidwe aku kalalika Mawu a Mulungu. Uwu ndi undindo wa moyo wake wonse munthu chifukwa cha ichi munthu sapita kukawonjezeretsa nthawi ya makalata kapena chiphatso chake chaka ndi chaka. Munthu woti adzozedwe akhale kuti wamaliza maphunzilo omukonzekeletsa ntchito ya utumiki. Akhale munthu wokhwima mu uzimu, wa mphatso zauzimu ndi wobala zipatso mu ntchito ya utumiki. Ndi zotero kuti anthu odzozedwa adzapereka mphamvu zawo zonse ku utumiki wa ntchito ya Ambuye nthawi zonse masiku amoyo wawo.

Munthu amene ali ndi chiphatso kuti adzozedwe, achite zinthu izi:

1. Kumaliza maphunziro ofunikira a anthu odzozedwa.

2. Akhale woti watumikilapo ali ndi chiphatso kwa zaka zitatu zotsatizana kapena zaka zinayi (4) ngati ali wachiwiri kwa abusa.
3. Akhale kuti wachitiridwa umboni ndi a komiti ya tchalitchi kapena Bungwe La Alangizi a Chigawo kuti chiphatso chake chiwonjezeredwe nthawi.
4. Bungwe La Chigawo Losungitsa Mwambo mu Mpingo limufufuze ndi kumuwona kuti avomerezedwe.
5. Ngati ndi woti banja lake lidatha; Bungwe La Atsogoleri A Akulu A Mpingo Wonse lidzawona ngati kuli koyenera kuti muthuyo adzozedwe - kapena ayi.
6. Munthu amasankhidwa kuti adzozedwe ndi mavoti oposa theka ku msonkhano wa chigawo.
7. Mwambo wa kudzoza abusa ndi mwambo wapaderadera womwe amachititsa ndi Mtsogoleri Wamkulu Wa Mpingo Wonse pa msonkhano wa pachaka wa chigawo. Mtsogoleri Wamkulu Wa Mpingo Wonse pamodzi ndi abusa ena odzozedwa amene alipo pa nthawiyo amaika manja awo pa munthuyo ndi kumudzoza ngati mbusa kapena dikoni mu Mpingo wa Nazarene.

Kubvomereza Ziphaso za Abusa Ochoka ku Mipingo Ina (432)
Abusa odzozedwa ochokera ku mipingo ya chi Evangeliko ofuna kuti atumikire mu mpingo wa Nazarene achite zinthu izi:

1. Alembe mayeso okhudzana ndi Buku La Malamulo Ndi Mayendetsedwe A Mpingo Wa Nazarene ndi Mbiri ya Mpingo wa Nazarene.
2. Ayankhe mafuso amene amaperekedwa kwa anthu ofuna kudzozedwa.
3. Akwaniritse zinthu zonse zomwe tatchula kale.

Zikatelo Mtsogoleri Wamkulu Wa Mpingo Wonse adzapereka satifiketi kwa munthuyo yosonyeza kuti walandiridwa mu mpingo wa Nazarene.

Kusiya Kapena Kuchotsedwa pa Ubusa
Udindo wa mbusa ndi wachikhalire chifukwa sachita kulira kuwonjezeretsa nthawi ayi, komabe mbusa amayembekezedwa kuti azipereka lipoti la ntchito yake ku msonkhano wa pa chaka. Satifiketi yomwe munthu amalandira atamudzoza imakhala ngati pangano pakati pa Iyeyo ndi mpingo. Panganoli limakhala ndi mphamvu ngati moyo wake ndi chiphunzitso chake zili zogwirizana ndi ziphunzitso ndi makhalidwe a mpingo.

Abusa odzozedwa sadzaloledwa kukonza mapulogalamu pa tchalitchi womwe si ali mu ndondomeko ya mpingo wa Nazarene, popanda chilolezo cha Adivaizale Komiti.

Mbusa kapena Dikoni akalowa mpingo wina, ndiye kuti sadzakhalanso Mbusa kapena Dikoni wa Mpingo wa Nazarene. (433.10)

Mbusa akhonza kusiya ntchito ya utumiki ndi kukabweza makalata ake ku distilikiti imene ikatumize makalatawo kwa Mlembi Wamkulu Wa Mpingo Wonse kuti asunge. (435.10)

Mbusa amene wakhala zaka zokwana zinayi (4) asanapatsidwe tchalitchi, akhonza kuikidwa mu Gulu la abusa osiya ntchito ya utumiki, ndi adistilikiti. (436.2)
Machitidwe a nkhani yonena za mbusa amene sakuyenda bwino alembedwa mu Buku La Malamulo Ndi Mayendetsedwe A Mpingo Wa Nazarene 505-507.2.

Mawu a Mulungu kwa Abusa ndi Atsogoleri a Mpingo
Mtumwi Paulo adati kwa akulu a mpingo a ku Aefeso, “Tadzichenjerani nokha ndi gulu lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuikani oyang’anira, kuti muwete Eklesia wa Mulungu, amene anamugula ndi mwazi wa Iye yekha” Machitidwe 20:28

Mtumwi Petro adati, “Wetani gulu la Mulungu liri mwa inu, ndi kuliyang’anira, osati mokakamiza koma mwaufulu kwa Mulungu;

osatsata phingu lonyansa, koma mwachangu. Osati monga achita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo. Ndipo pakuwonekera Mbusa Wamkulu, mudzalandira korona wa ulemelero, wosafota" (1Petro 5:2-4)

Mpingo Wa Nazarene
Ngodya Za Zikhulupiriro

Kuyanjananso ndi Mulungu

Kulungamisidwa, Kubadwanso Mwasopano, Kukhalanso Mwana wa Mulungu

Chiyeretso Chathunthu



Kubweranso Kwachiwiri Kwa Khristu

16

Chiukitso, Chiweruzo, Kokhala Muyaya